


# AHEBRI, MUTU WACHITATU

 Mmawa wabwino, amzanga. Ndi mwayi kuti tiri pano mmawa uno mu utumiki wa Ambuye. Ndipo ife tikuyembekeza ndi kudalira kuti kukhala nthawi yaikulu.

<sup>2</sup> Ine ndinali basi mmbuyo...yomwe ife tinkaitcha ofesi ya madikoni, komwe kuli marekoda tsopano, ndipo ndinali kungoyankhula ndi dona wamng'ono ndi mayi ake kumbuyo uko, ochokera uko ku Joliet, Illinois. Ndipo ine ndimangolingalira chobalidwa cha chisomo cha Mulungu chomwe msungwana uyo ali. Ambiri a ife kuzungulira kuno tikumudziwa iye. Iye ndi—chidakhwa, mtundu umodzi woyipisitsa. Ndipo ine sindinaimve nkhaniyo momveka kwa ine mpaka mmawa uno, momwe kuti pamene iye anachoka pa nsanja. Ambuye ataulula kwa iye zonse zomwe zinali zolakwika ndi zomwe zinali zoti zikachitika. Ndipo iye anachoka pa nsanja, akulira ndi kusangalala chifukwa Mulungu anali atamupulumutsa iye k—ku manda auchidakhwa. Ndipo iye...Dona anayenda napita kwa iye ndipo anayamba kulira, kuti mwana wake wamkazi, ine ndikukhulupirira iye anali, anali wa chibaba cha zozunguza mutu. Ndipo inu mukudziwa, mwa chisomo cha Mulungu, msungwana ameneyo anaitanidwa. Ine ndikukhulupirira, unali usiku wotsatira, Rosella anaitanidwa. Ndipo msungwana wochokera ku zozunguza mutu anachiritsidwa. Ndipo iye ndi mwamuna wake akulalikira Uthenga. N—n—ndipo kumuwona dona wamng'ono wokonedwa monga Rosella, ndipo atakhwima basi. Ndipo tsopano iye, ndi wolemekezeka kwambiri, iye ali...akumverera kuitana mu mtima mwake. Koma, podziwa Baibulo pa za alaliki achikazi, mukuona, iye akudziwa kuti ndi chinachakenso. Ndipo Mulungu akumutsogolera iye kukalowa mu ndende ndi zinthu, kumakapakereka umboni.

<sup>3</sup> Ndi zodabwitsa basi k—k—kudziwa, kufunafuna chifuniro cha Mulungu. Nthawizina ife timakhala nako kumverera, koma ife timafuna kuti tikutengere kumverera uko mu malo; ngati iwe sungasamale, Mdierekezi angatenge kumverera uko ndi kukupotozera iko mu chinachake. Koma bola ngati ife tikukhala mu Baibulo, ndiye ife tikulondola, inu mukuona, ife tikuyenda limodzi ndi chifuniro cha Ambuye.

<sup>4</sup> Ndipo kotero ine ndikukhulupirira k—kuti Rosella potsirizira atembenukira ku minda ya utumwi kwinakwake, chifukwa Amereka sakuwufuna Uthenga.

Inu mukudziwa izo. Ife tikhoza kungovomereza izo, kuti, anthu Achingezezi Achisaxoni awa, iwo atha. Ndizo zonse. Palibenso Uthenga umene Amereka ati adzaulandire. O, inu

mumangopeza ozandimiramo pang'ono, pano ndi apo. Koma, tikangonena za Uthenga, iwo watha. Ndipo inu simungakhoze kulalikira nkomwe kwa iwo, simungakhoze kuyankhula nkomwe kwa iwo. Iwo sangakhoze kukhulupirira kanthu. Mukuona? Iwo angokhala ndi malingaliro awo awo amutu wowuma, ndipo iwo akhazikika.

Ndipo zinthu zotsatira kwa fuko lino ndi chiweruzo. Ilo lidzakhala nacho icho, naponso. Icho chikhoza kukhala kupyolera mu kugwa kwa chuma. Izo zikhoza kukhala kupyolera mu bomba la atomiki. Izo zikhoza kukhala kupyolera mu mliri waukulu, nthenda kapena chinachake. Koma, icho chakonzeka. Icho chikubwera. Zikwi kuphatikiza zikwi zidzagwa.

<sup>5</sup> Ife timadutsa uko, dzulo, M'bale Zabel ndi ine, kwa . . . ndi M'bale Woods, tikubwera kuno kuchokera uko ku Kentucky, komwe ife tinakhala tiriko kwa masiku atatu, ndipo ife tinadutsa pafupi ndi ntchito yomanga manyumba. M'bale Zabel anati, "Palibe . . ." Ine ndaiwala. "Palibe nkomwe aliyense wa anthu awo, mu ntchito iyo, omwe amapita ngakhale ku mpingo uliwonse."

<sup>6</sup> Inu mukhoza kuwafunsa iwo za izo. "Chabwino, ife tiri nayo televizioni yathu. Ndi pomwe ife timapezera chitonthozo chathu." Mukuona? Ndilo khalidwe la Achimereka. Mukuona? "Ife tiri ndi televizioni. Ife tiri nazo ndalama zambiri. Ife tiri nawo magalimoto abwino, tiri ndi manyumba abwino. Ife tikusowa chiani kwa Ambuye? Ife sitikusisowa Zimenezu." Ndilo khalidwe lawo.

<sup>7</sup> Pafupi za chipembedzo chokha ndi chipulumutso chomwe ife tiri nazo, ndi chikondi, ziri pakati pa anthu aumulungu enieni. Inu mukudziwa, Baibulo linanena kuti izo zikanadzachitika. [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.] A—nha. Inu owerenga Baibulo, ine ndinakumvani inu mukufuula "ameni," ndi inu alaliki kumbuyo uko. Izo, ndiko kulondola. Chikondi chidzakhala chiri kutali kwambiri choncho, mu masiku otsiriza; chikondi chokha chomwe chiti chidzatsalire, chidzakhala pakati pa Osankhidwa a anthu a Mulungu. "Bambo adzakhala motsutsana ndi mayi, ndi amayi motsutsana ndi bambo, ndi ana motsutsana ndi makolo, ndi osiyanasiyana azidzatsutsana wina ndi mzake." Ndipo chikondi chokha chomwe chiti chidzatsalire, chidzakhala chiri icho cha Osankhidwa okha, Osankhidwa okha. Mawu oti "Osankhidwa" apo akuchokera ku mawu okuti "Wosankhidwa," anthu osankhidwa ndi Mulungu.

<sup>8</sup> Ndipo pamene Rosella amawerenga mobwereza nkhanio kwa ine mu chipinda, kanthawi kapitako, ine ndinali kungogoniza, kuti, pa usiku umenewo, iye anati chinachake chinachitika. Ndi momwe anati, kudutsa mu moyo wake wonse, pamene iye ankangokhala ali chidakhwa cha maso otchingika. Sizikanakhoza, Othandizira Zidakwa. Madotolo

anayi anamulephera iye. Palibe chimene chikanakhoza kuchitidwa. Ndi momwe, kuchokera pa mphindi iyo yomwe, chinachake chinachitika.

<sup>9</sup> Tsopano iye sali wa maso aphephethi aja. Iye ndi msungwana wamng'ono, wokonedwa, wokongola wa usinkhu wa zaka sate-firii, ndipo angapambane ngati wa pafupi twente-thuu; basi momwe Mulungu anamuchitira iye zomwe Iye anachitazo, ndi momwe iye akuwonekera mosiyana. Ndipo, koma ine ndinati, “Rosella, asanaikidwe maziko a dziko, Mulungu anadzozeratu mphindi imene ija.” Inde, bwana. Mukuona? Kulondola. Ndipo pamene Billy Paul wamng'ono uyo kumbuyo uko, komwe iye ali, pamene anali kupereka makadi apemphero kwa anthu usiku umenewo, momwe iye ankadziwira mochepa yemwe iye anali kumupatsa khadi lapempherolo.

Si zodabwitsa izo, Rosella?

[Mlongo Rosella Griffith akuti, “M'bale Branham, ine ndikudabwa ngati mpingo ungapemphere kuti Mulungu azititsogolera ife, momwe Iye analiri wamphamvu.”—Mkonzi.]

Ameni. Ambuye akudalitse iwe, Rosella. Ine ndikutsimikiza ife tichita zimenezo. Iye akufuna kuti mpingo upemphere kuti Mulungu azimutsogolera iye. Ndiko, kutsatira dzanja Lake losasinthu. O, izo nzabwino kwambiri.

<sup>10</sup> Ndinali ndi kusankha kovuta komwe kunaikidwa patsogolo panga, mmawa uno. Ndi zokhudza ena, amamilioni kuchulukitsa kangapo kuchulukitsa kangapo omwe akufuna kuti apereke kuno ku Louisville, Kentucky, ndi kundimangira ine kachisi wa madola mamilioni asanu. Koma chinachake pansu mu mtima mwanga chinati, “Dikira kaye, iwe sindiwe m'busa.” Mukuona? Koteru, ndiye, ndalama zokwana madola mamilioni asanu zomwe zikanati zidzaikidwepo. Tsopano amachita kupita ku boma, ndi kukalipira mowa ndi zinthu zonga izo, koma akufuna kuti aziyike izo ku kachisi wa Ambuye. Koma ine ndikuyembekeza kuti izo zipita kwa wantchito wina wa Mulungu yemwe ati...ndi utumiki wina wa Mulungu. Koma, awo ndi madola mamilioni asanu omwe aperekedwa tsopano. Taganizani za izo, angakhale kachisi wotani zomwe izo zikanadzapanga.

Ukuona kukongola kwake momwe izo zikuwonekera, Rosella? Koma pali chinachake mmusi *umu* chimene chikunena mosiyana. Mukuona? Mukuona? Chinachake mmusi *umu*.

<sup>11</sup> Ife timabwera mu kachisi, wamng'ono wakale uyu, inu alendo. Chabwino, awa akanakhoza kukhala malo onyezimira kuno pa ngodyayi, inu simukuzindikira zimenezo, kuti anthu akhala akufuna kuti amange malo awa ndi kuwapanga iwo. Koma umu ndi momwe ife tikuwakondera iwo. Mukuona, umu ndi momwe ife tikuwakondera iwo. Mipando yakale yomwe ife tinkakhalapo uko, inali—mipando yapachiyambi kuchokera

mu kachisiyo kuno, inapita kupyola mu kusefukira ndipo inayandama mmwamba.

<sup>12</sup> Baibulo langa liri chitsegulire monga *choncho* pa guwa. Ilo linakakanilira ku denga ndipo linabwerera pansi ndi Mawu pa Ilo, “Ine Ambuye ndinabzala izo. Ine ndizitsirira izo usana ndi usiku kuwopa kuti ena angazikhwathule izo kuchokera mu dzanja Langa.” Momwe ife tinapalasira pamwamba pa iye ndi choyandamira, *muno*. Ndipo ilo linabwerera pansi pomwe, mipando kusunthira kubwera ku malo ake omwe. Zonse zomwe iwo anachita zinali kungoitsulukuta ndi kumapitirira nazo. Mukuona? Mukuona? Kotero umu ndi momwe ife tikuzikondera izo, komwe kuli anthu wamba, malo a wamba, ndi Ambuye wodabwitsa. Amen.

<sup>13</sup> Tsopano, lero, ife tiri nazo zina, ife tikungoyamba kumene kuti tilowe mu zonona, inu mukudziwa, pambuyo poti—mkaka wonse utachotsedwapo, ndi zonona basi. Ndipo kumbukirani, zimatengera mkaka kuti upange zonona, inu mukudziwa. Z—zononazo ndi zamkati mwa mkaka.

<sup>14</sup> Kotero ife takhala tiri mu wa 1, wa 2, ndipo ife tikutsirizira mu wa 3, ndi kuyamba mu mutu wa 4 wa Bukhu laulemerero la Ahebri. Ndipo, o, ziphunzitso za Bukhu ili! Ife tikhoza kukhala nalo Ilo, pa ndime imodzi, kwa miyezi itatu, ndi kumangosonyeza kuti Baibulo lonse likumangirizira mu ndime iliyonse mu Baibulo. Kodi inu munayamba mwalingalirapo za izo? Palibe ndime imodzi yomwe inu mungakhoze kuikapo chala chanu, koma yomwe, mwa chisomo ndi thandizo la Mzimu Woyera, ife tingakhoze kumangiriza Genesis mpaka Chivumbulutso mpaka kwa Iyo yomwe.

<sup>15</sup> Palibe chidutswa china cha zolembedwa chinalembedwa kulikonse chomwe chingakhoze kuchita izo. Ndipo mwamasamu, ndi mwachirengedwe, mwa njira iliyonse, kulibe Bukhu mu Baibulo linalembedwa monga Baibulo... Kulibe bukhu mu dziko, ine ndikutanthauza, linalembedwa monga Baibulo. Kulibe lina. Ziwerengero za m’Baibulo ndi zangwiro mu chiyanjano; basi ngakhale mitu, ndi zopumirira, ndi chirichonse, ndi zangwiro. Palibe bukhu lina; iwe sungakhoze kuwerenga mutu kuchokera mmenemo popanda kudzibweza lokha mmbuyo. Koma mulibe kupingana kumodzi mu Baibulo lonse. Ndipo linalembedwa ndi anthu ambiri, ambiri mbiri; ndi mazana, ndi mazana, ndi mazana a zaka motalikana. Mosadziwa chidutswa chimodzi; mmodzi ankalemba Ilo *kuno*, ndi wina ankalemba Ilo *kuno*, ndi wina ankalemba Ilo cha *kuno*. Pamene Ilo lonse linapangidwa pamodzi, Ilo linapanga Baibulo la Mulungu. Ndipo palibe limodzi limatsutsana ndi limzake lina, ndipo, palibe, masamu, mwachirengedwe. China chirichonse cha Baibulo, chirichonse, ziwerengero, chirichonse chimayenda mwangwiro malimodzi. Izo osakhala zowuziridwa,

ine sindikudziwa, kodi inu mukanatcha chiani kudzoza? Ndine wokondwa kwambiri chifukwa cha Baibulo lakale, lodala.

<sup>16</sup> Ena a iwo anati, “Kodi ndinu Mkatolika? Mprotestanti?”

Ine ndinati, “Si mmodzi wao. Ine ndimakhulupirira Baibulo.” Ndiko kulondola. Ine ndimakhulupirira Baibulo, ndipo ndine wokondwa kuti ife tikadali nawo ufulu woti tizililalikira Ilo mu fuko lino. O, Ndi zodabwitsa.

<sup>17</sup> Tsopano ife tikuti tiphunzire kuchokera mu Ilo. Ndipo tsopano ife titembenuzira mu Bukhu la Ahebri ndi kuyambira ndi mutu wa 3. Ndipo ife tinalekezera pa ndime ya 15. Ndipo tsopano inu nonse. . .

<sup>18</sup> Ine ndinamuwona winawake anazindikira, kanthawi kapitako, pamene ine ndimakatenga magalasi anga owerengera. Izo sikuti maso anga ali moyipa, koma ine ndadutsa usinkhu wa zaka forte. Ine ndikanakhoza kuziwerenga izo, *apa* pomwe, mwawamba chabe, koma ine ndikhoza kuwerenga izo mwabwinoko ndi magalasi. Ndipo iwo andipangira ine magalasi owerengera omwe ine ndikufuna kuti ndiziwagwiritsa ntchito, chifukwa ine ndikhoza kumawerenga izo mwabwinoko ndi mofulumirako. Ndipo ndi chifukwa chomwe ine ndinawapezera iwo. Tsopano mu. . .

<sup>19</sup> Poyamba, ife tikufuna maziko pang’ono, chifukwa pakhoza kukhala alendo ena pakati pathu, omwe sanaligwire gawo loyamba la Bukhu la Ahebri.

<sup>20</sup> Kodi ndinu Akazi a Cox, mwakhala apa pomwe pa mapetopo? Chabwino, ine ndikukondwa motsimikiza powawona iwo, basi ine ndisanati ndiyambe, ngati umboni kwa chisomo cha Mulungu. Apa pali mkazi anali ndi khansara ikumudya nkhope yake yonse. Amenewo ndi amayi awo a Mlongo Wood. Ndipo ine ndinali ku Michigan ndi Gene ndi Leo, ndi iwo, akutenga zojambula. Ndipo tiri pa njira wakwathu, mkazanga anandiimbira ine, kapena ine ndinamumbira iye. Iye anati, “Pita ukapemphere pompano chifukwa Akazi a Cox, mayi awo a Akazi a Wood, pakuti khansara ikudya nkhope yawo yonse.” Yapita kale kumbali ya diso ndi mpaka ku fupa, yakhathamira ku mbali ya nkhope yawo, ndipo ikungomwazikana. Dotolo wina anachita chinachake kwa iyo, anangoipangitsa iyo kuipira, ndipo basi anangoimwaza iyo; anaika mtundu wina wa mankhwala mmenemo.

<sup>21</sup> Ndipo iwo anamubweretsa iye kuchokera uko ku Campbellsville, Kentucky, mpaka ku. . .kapena, ine ndikukhulupirira, Acton, Kentucky, mpaka k—ku Louisville, kukalandira chithandizo.

<sup>22</sup> Ndipo kotero Akazi a Woods, nthawi yoyamba yomwe ine ndinawawona iwo konse nkuti iwo anali atasweka mtima. Chifukwa, ndithudi, ndi a—amay—awo, ndipo zedi iwo akanakhala akumverera kusweka mtima. Ndinapita mu

chipindamo ndipo ndinakawapempherera iwo, ndi chidaliro kuti Mulungu anati Iye aziyankha pemphero. Ndipo masiku angapo, iwo anali atatuluka. Ndipo apo iwo akhala tsopano. Ndipo basi ndi chisomo chodabwitsa, momwe Iye wawachitira iwo.

<sup>23</sup> Kodi inu mungati muime? Ine sindikufuna kuti ndikupangeni inu c—c—chapagulu...Pati, ndi pati pamene khansayo inali? P—pa mbali ya nkhope yawo, mukuona apo, pa mbali *iyoy* ya nkhope yawo, kutsika kuzungulira *apa*, mpaka ku fupa la chibwano chawo, kukwera kuzungulira diso lake. Ndipo Mulungu wawachiza iwo. Kodi Iye si wodabwitsa? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.]

<sup>24</sup> Ndi angati anali pano Lamlungu latha kuti anawona chomwe Ambuye anachita mwa masomphenya? Bambo, zonse wolumala ndi wakhungu, atakhala apo pomwe mu chikuku. Ndipo chinachake chinandipweteka ine pamene bambo wachikulire uyo anali atakhala apo nati, “M’bale Branham...” Ine ndikukhulupirira anali m’bale uyu apa pomwe. Anati, “Mukawachitire chinthu chomwecho akazi anga.” Iye ali ndi mkazake pano yemwe ali wolumala. Mtima wanga unangosungunuka. Ine ndikukhumba... Ine ndikanamapereka chirichonse mu dziko ngati ine ndikanatha, koma izo si... si ziri mu mphamvu zanga. Koma izo ziri mu mphamvu zanga ndi mphamvu zanu, kuti tizipemphera kuti Mulungu azichita izo. Iye ali ndi mkazi wolumala, dzanja lopuwala, phazi lopuwala, zikuwoneka ngati. Ndipo bambo uyu anali moyipa kwambiri kuposa iye, chifukwa iye akhoza kuimirira ndipo akhoza kuyenda pang’ono, koma bambo uyu sakanakhoza ngakhale kuchita izo. Ndipo iye... Ubongo, msempha weniweni wokuyimitsa unali utapita. A Mayo, ochuluka enanso, anali atomulephera iye. Ndipo Wachikatolika anamutumiza iye kuno, dotolo wa Chikatolika; ndipo mnyamata wake ndi wansembe ku St. Meinrad kumeneko mu Jasper, Indiana. Koma uko ndi kuika miyala ya maziko kwa chitsitsimutso icho chomwe chikudzapo, kumeneko.

<sup>25</sup> Ndipo pamene iye anaukapo, iye anati, “Koma ine sindingathe...” Iye anayang’ana, anati, “Inde, ine ndikhoza.” Iye ankaganiza kuti iye sakanatha kuwona, inu mukudziwa. Ndipo iye anayang’ana mmwamba, ndipo anangopezeka kuti amakwezera mutu wake mmwamba, ndipo apo iye amakhoza kuyenda ndi kupenya; anayenda kutsika ndi mpita uwo, mwa yekha. Ndipo iwo anali Achipresbateria. Iye anali wa chiorthodox. Ndipo kunena... Inu mukuganiza kuti ndi Achipentekoste okha kapena anthu a Chiyero omwe angakhoze kufuula; inu mwalakwitsa. Iwo akhoza ndithudi kuchitapo kufuula kwina pamene iwo awona chinachake chonga izo zitachitika; kukumbatirana wina ndi mzake ndi kumafuula. Anayenda akutuluka ndi kumatsika masitepewo, akukankha chikuku chake; akuyenda, ndi msempha wokuimika utachoka

mmutu mwake. Taganizani za izo. Akuyenda monga momwe inu kapena ine tingayendere. O, Iye ndi wodabwitsa.

<sup>26</sup> Tsopano, Paulo analemba Bukhu la Ahebri. Ndipo mu kulemba uku kwa Ahebri, iye analilemba Ilo. Ndipo Iye asanawalembe Mabuku awa...Ife tikupeza tsopano. Ife tikuti...Ili ndi kalasi la Sande sukulu, ndipo ine ndiyesera kuti ndiziyang'ana ndipo sinditenga motalika kwambiri. Ndiyeno ife tikhala ndi misonkhano, kuti tidzapitirize izo usikuuno, Ambuye akalola. Tsopano, mu Bukhu la Ahebri ndi Makalata ena onse a Paulo...

<sup>27</sup> Paulo anali ndani? Iye anali M'hebri wolimba, sikolala, ndi mphunzitsi wamkulu wa Chipangano Chakale. Ndipo iye anali ataphunzitsidwa ndi mmodzi wa amuna opambana a tsiku lake. Winawake andiuze ine lomwe linali dzina lake. Gamalieli, mmodzi wa aphunzitsi akulukulu a tsiku lake. Ndipo Paulo anali atakhala pa phazi la Gamalieli.

<sup>28</sup> Pali chinachake cha k...kumene iwe umapita, mpingo umene iwe umapitako, ndi mphunzitsi yemwe amakuphunzitsa iwe. Kodi inu mumadziwa zimenezo? Izo, izo ziri ndi chinachake kwa izo. Chotero ife timayenera kuti tizifunafuna opambana kwambiri omwe ife tingathe kuwapeza, kotero ife tizipeza zopambana; osati chifukwa ndi wachitukuko ndi zina zotero, koma kuphunzitsa kwenikweni kwa Baibulo.

<sup>29</sup> Penyani, nthawi ina pamene Israeli anafika mu chipululu ndi ankhondo awo, ndipo iwo anali ndi msasa wa masiku asanu ndi awiri, ndipo madzi anawathera. Ndipo iwo anali pafupi kuwonongeka, iwo anati, "O, ngati kukanakhala mneneri pafupi!"

<sup>30</sup> Ndipo mmodzi wa iwo anati, "Ife tiri naye kumusi kuno, Elisha. Iye ankatsanulira madzi pa manja a Eliya." Mukuona woyanjana nayeyo? Mwa kuyankhula kwina, "Apa pali Elisha yemwe anakhala nacho chiyanjano ndi Eliya. Mawu a Ambuye ali ndi iye." Inu mukumvetsa izo? Iye anali ataphunzitsidwa molondola. Ndipo iye anati, "Iye ali kuno. Tiyeni tipite uko ndi kukamufunsa iye, chifukwa mphunzitsi wake anali Eliya, ndipo iye ali nako kuphunzitsa kwa Eliya mwa iye." Mukuona kusiyana komwe izo zikupanga? Zedi. Ife timafuna kuti tiziphunzitsidwa.

<sup>31</sup> Kotero, Paulo anali nako kuphunzitsa kwa Gamalieli. Ndipo Gamalieli anali munthu wamkulu uja yemwe anapanga kusankha, pokhala sikolala iyemwini, kuti pamene kutengeka konse uku kwa mpingo woyambirira kunayamba, iye anati, "Tiyeni tisaike manja athu pa izo, abale. Ngati izo siziri za Mulungu, izo sizifika ku kanthu, mulimonse. Koma ngati izo ziri za Mulungu, ndipo ife tikamamenyana nazo, ife tidzipeza tokha tikumenyana ndi Mulungu." Mukuona, iye anali ndi kuphunzitsa kwina kwabwino.

<sup>32</sup> Paulo anali atabwerapo pansi pa bambo uyu, ndipo iye ankadziwa kuti Paulo anali mphunzitsi wamkulu. Koteru, tsiku lina, woota mu mtima, akuwuzunza Mpingo, akupita uko kuti akawamange iwo.

<sup>33</sup> Tsopano tiyeni tingotenga gawo lina laling’ono kuchokera kwa Paulo, pamene ife tikuika maziko athu.

<sup>34</sup> Pamene Yudasi anagwa, mwa cholakwira, mwa chikondi cha ndalama ndi kunyada kwa moyo, iye anagwa nachoka ku chisomo ndipo anapita ku malo ake. Ndipo ophunzira anati, “Payenera kukhala khumi ndi awiri.” Ndipo mpingo, ndi upamwamba wake wonse, kuti azikusonyezani inu chomwe mpingo uli; ndi upamwamba wake wonse ndi mphamvu zake zonse, iwo ukadali mailosi milioni woperewera, mwa kuchita kwake kwabwino kwambiri. Iwo anati, “Ife tiyenera kuti tiyang’anepo, mmodzi pakati pathu, yemwe ati atenge malowo.” Ndipo iwo anasankha, mwa kuponya voti, Matiya. Matiyasi, ine ndikukhulupirira, kapena Matiya. Matiya, ine ndikukhulupirira ndi yemwe ali. Ndipo pamene anamusankha iye ndi kumuika iye limodzi ndi khumi ndi awiriwo, limodzi ndi khumi ndi mmodzi, chomwe chimapangano khumi ndi awiri, iye sanachite chinthu chimodzi. Iyo ndi nthawi yokha yomwe dzina lake linatchulidwa konse mu Malemba. Uwo unali mpingo kupanga kusankha kwake.

<sup>35</sup> Tsopano, iwo anaganiza, “Iye ndi njonda.” Palibe kukaikira. “Iye ndi munthu wodabwitsa. Iye ndi sikolala. Iye ndi wanzeru. Iye ndi wophunzira. Iye ndi munthu wodabwitsa. Iye angawatenge malo a Yudasi ndi kukhala mmodzi wa ife.”

<sup>36</sup> Koma, inu mukudziwa, Mulungu nthawizina amapanga zina za . . . kwa malingaliro athu, kwina kwa kusankha kopusa kwambiri. Tsopano, Mulungu anamuwona Myuda wina wamng’ono wa mphuno-yangowe, wodzaza ndi kupsya mtima monga iye akanati akhalire, ndi kamwa yake yoyikidwa cha mbali, “Ine ndipita uko, ndi kukamanga aliyense wa iwo. Ine nd—ine ndikawaponyera iwo mu ndende. Ine ndikachita izi.” Uyo anali kusankha kwa Mulungu.

Onse a iwo anatenga sikolala ndi nthumwi. Uko ndiko kusankha kwa mpingo.

<sup>37</sup> Mukuona, inu simukudziwa yemwe uyo ali pa guwa. Inu simukudziwa yemwe uyo ali inu mukumuchitira umboniyo, mu ndende kapena kulikonse komwe kuli. Izo zikhoza kuwoneka ngati wankhonya, makutu ake atasweka, maso atasupulidwa, ndipo, koma inu simukudziwa yemwe uyo ali. Inu mungoponya maere anu, ndizo zonse, mupatseni iye Mawu. Mulungu amatenga kusankhako.

<sup>38</sup> Ndipo Mulungu akumusankha Myuda wamng’ono wopsya-mtima uyu, kapena anamusankha iye, kani. Ali pa msewu akupita, “Ine ndipita uko ndi kukawatenga iwo. I—ine



ndiwasonyeza iwo chomwe ine ndingachite monga choncho,” ndipo Mulungu anangomugwetsera iye pansi.

Mulungu anati, “Uyo ndiye womsankha wanga, apo pomwe.”

<sup>39</sup> Kodi izo sizikanati zikhale zopusa, kwa mpingo? “Bwanji, iye akuwuzunza mpingo. Iye ndi munthu wachithupithupi.” Koma Mulungu ankadziwa chomwe chinali mkati mwa munthuyo. Mukuona chimene ine ndikutanthauza?

<sup>40</sup> Chotero, Paulo anali nacho chomuchitikira. Ndi angati akukhulupirira kuti chokuchitikira chimabwera ndi kutembenuka? Zedi. Ngati izo sizinatero, ine ndikanakaikira kutembenukako. Kutembenuka kumabweretsa chokuchitikira. Ndipo inu simungakhoze kuziyika izo kwa chirichonse tsopano. Nthawizina izo zikhoza kukhala kufuula. Nthawizina izo zikhoza kukhala kuyankhula ndi malirime. Nthawizina izo zikhoza kukhala kulira. Nthawizina izo zikhoza kukhala kubuula. Inu simukudziwa chomwe icho chiri, kotero musamayesere kuziyikapo izo. Chifukwa, aliyense wa inu wapezeka kuti akulakwitsa mu zimenezo, inu Amethodisti, ndi inu Abaptisti, ndi inu Anazereni, ndi Achipentekoste.

<sup>41</sup> Ine ndawawonapo anthu akufuula molimba basi momwe iwo angafuulire, ndi kukubera golide kuchokera pa mano ako, iwo akanakhoza. Inde, bwana. Ine ndawawonapo anthu akuyankhula ndi malirime ngati akutsanulira nandolo pa chikopa chang’ombe chowuma, n—ndipo owonamtima ndi abwino, akutafuna fodya ku mbali ina ya kamwayo, ndipo angadule khosi lako ngati iwo akanakhoza kuchita izo. Ndiko kulondola. Chotero zinthu zimenezo zilibe... Palibe umboni ayi womwe inu mungakhoze kutsimikizira izo, kokha mwa moyo umene munthuyo akukhala. “Ndi chipatso chawo, inu mudzawadziwa iwo.”

<sup>42</sup> Kotero, zonsezo ziri kwa Mulungu. Iye amapanga kusankha. Iye amabweretsa zinthuzo pamodzi, ndipo umo ndi momwe izo ziriri. Kotero ngati moyo wanu ukufanana ndi zipatso za Baibulo, inu muli ndi kumvetsa kwabwino kwambiri. Ngati mzimu wanu ukuchitira umboni ndi Mzimu Wake, kuti ndinu ana aamuna ndi aakazi a Mulungu, inu muli... Ngakhale, choipa chachokapo, ndipo chirichonse chakhala chatsopano, ndipo inu mukukhala mu chikondi, ndipo inu muli nawo mtendere, ndi chisomo, ndi zina zotero, inu mukuyandikira kwambiri ku Ufumu ndiye. Chifukwa, Moyo umene uli mwa inu ukubala moyo wa mtundu umenewo. Mukuona?

<sup>43</sup> Ngati inu muti, “O, aleluya, ine ndinayankhula mu malirime. Aleluya!” Izo sizikutanthauza kanthu. Izo sizikutanthauza pang’ono mochuluka ngati inu mukanapita kunja kuno ndi kukaimba nyimbo pa gitara kapena chinachake. Izo sizimatanthauza chinthu chimodzi. Ngakhale inu mutayankhula

ndi malirime, ngakhale inu mutafuula, ndi kuthamanga chokwera-ndi-chotsika mu kampata, ndi kulira misonzi ngati kuti inu mumasenda anyezi, izo sizikunthauza chinthu chimodzi, osati chinthu chimodzi, kupatula ngati moyo wa tsiku lililonse ukuikira kumbuyo chimodzimidzi basi, ukukhala ndi Iwo.

<sup>44</sup> Tsopano, ngati inu mukuchita zinthu zimenezo, kuphatikizira moyo umenewo, “ameni,” izo, nzabwino. Izo ndi zabwino. Koma inu mukhoza kumachita zinthu zimenezo popanda kukhala ndi moyo umenewo.

<sup>45</sup> Kotero ndiye, osati kufuula, osati kanthu kena konga izo kali umboni. Yesu anati, “Ndi chipatso chawo, inu mudzawadziwa iwo.” Ndipo chipatso cha Mzimu si kuyankhula ndi malirime. Icho si chipatso cha Mzimu. Kufuula si chipatso cha Mzimu. Kulira si chipatso ichi cha Mzimu. Koma, chikondi, chimwenwe, mtendere, kupirira motalika, ubwino, unjonda, chikhulupiriro, kufatsa, kudziletsa, ndizo zipatso za Mzimu. Mukuona? Ndizo zomwe ziri zipatso za Mzimu. Chabwino.

<sup>46</sup> Tsopano, chifukwa chomwe ife tiri nazo zinthu izi, iwo amakonda kupanga mabungwe, inu mukuona. “Chabwino, ife tizikhala nazo izo. Mulungu adalitsidwe, onse amakhulupirira momwe *ife* tikuchitiramu, ife tizipita njira *iyi*. Onse akukhulupirira momwe *ife* tikuchitiramu, ife tizipita njira *iyi*.” Koma Mulungu akufuna onse kuti azipita njira *Iyi*, mmwamba momwe.

<sup>47</sup> Tsopano, Paulo, atakhala nacho chomuchitikira ichi, ndiye iye anaganiza kuti icho chinali chomuchitikira chodabwitsa. Tsopano, motani...T—t—tiyeni tiwerenge mobwereza chomuchitikira icho pang’ono pokha. Paulo anali pa ulendo wake waku Damasiko, kuti akawamange anthu ena kumeneko, chifukwa Uthenga unali utafalikira kumeneko. *Uthenga* umatanthauza “nkhani yabwino.” Ndipo kotero iwo anabalalikira uko, ndipo anthu ambiri anali akuwukapo, odzala ndi chikondi, ndi chisangalalo, ndi kuwakonda Ambuye Yesu. Ndipo Iwo unali utafalikira uko mwanjira imeneyo. Chotero, Paulo anakatenga makalata ena kuchokera kwa Wansembe Wamkulu. Iye anati, “Ine ndipita uko, ndipo ndikawamanga iwo, aliyense.”

<sup>48</sup> Chotero iye anadzitengera gulu pang’ono la alonda, alonda a mkachisi, asilikari, njira yonse iwo anapita. Pamene iwo anali akuguba kutsika ndi msewuwo, ndipo iye akudziwa zonse zomwe akanati akachite, zonse mwadzidzidzi, chinachake chinachitika. Zonse mwadzidzidzi, apo panali Kuwala kwakukulu patsogolo pa iye. Kuwala Kwakukulu, tsopano, Iko kunawala ngati dzuwa. Ndicho chinthu chachilendo kuti chichitike. Kuwala kunawala mochuluka chotero kuti iye basi...Maso ake anatong’oka, pafupifupi. Ndipo anagwera

pansi. Ndipo i—iye ali pansi chigonere, ndipo iye anayang’ana mmwamba.

<sup>49</sup> Apo panali pafupifupi amuna khumi kapena khumi ndi asanu ali ndi iye. Kodi aliyense wa amuna awo anakuwona Kuwala kumeneko? Ayi, bwana. Paulo anakuwona Iko. Iko sikunakonzedwere kuti amuna awo akuwone Iko. Chotero, anthu ena akhoza kuwona zinthu, pamene, ena sangaziwone. Mukuona? Kotero, Paulo anakuwona Kuwala kumeneko, mochuluka chotero kuti Iko mpaka kunamuchititsa iye khungu. Samatha kuwona, kwa masiku angapo, Iko kunali chenicheni chotero kwa iye. Ndipo iye sankakhoza kupenya kwa angapo. . .

Kenako, pamene iye ankalemba makalata, maso ake ankamuvutitsa iye moyipa kwambiri kuchokera apo, mpaka iye ankalemba ndi zilembo zazikulu kwambiri. Iye anati, “Powona kuti ine ndalemba kwa inu ndi zilembo zazikulu.” Iye sankakhoza nkomwe kupenya.

<sup>50</sup> Iye anali ali mu ndende, ndipo iye anawafunsa Ambuye kuti amuchize iye kwa izo. Ndipo iye anafunsira kwa Iwo nthawi zitatu. Koma kodi Ambuye anati chiani? “Chisomo changa ndi chokwanira, Paulo.”

<sup>51</sup> Paulo anati, “Ndiye ine ndipezera ulemerero mu zifooko zanga.” Chifukwa, iye anati, “Kuwopa kuti ine ndingakwezedwe pamwamba pa kuchuluka kwa Vumbulutso, kunaperekedwa kwa ine mtumiki wa Mdierekezi, munga mu thupi langa, womwe unkanditunduza ine.” Iye ankakhoza kuchira kwa kanthawi, ndiyeno apo iwo amachokapo kachiwiri.

*Kutunduza* kumatanthauza “nkhonya pambuyo pa nkhonya.” Monga sitima pa nyanja, inu mukudziwa, mafunde amaitunduza iyo, mukuona, kumenya pambuyo pa kumenya.

Ndipo iye amakhoza, iye amakhoza kuchira, ndiyeno nkudzadwala nawo kachiwiri; kenako kukhala bwino, nkukhala nazo kachiwiri. Iye anati, “Ambuye, chavuta ndi chiani, Inu simukundichotsera ine izi?”

<sup>52</sup> Iye anati, “Chisomo changa ndi chokwanira, Paulo. Zingopitirira nazo.” Izo zikupangitsa. . .

<sup>53</sup> Iye anati, “Tsopano, n—ngati ine ndikanangokhala wangwiro basi, ndi chirichonse mwangwiro,” anati, “ndiye pamene ine ndimapitirira, o, ndikanamazitukumula ndi kumati, ‘Inu mukuona, palibe cholakwika ndi ine. Ambuye akundisamalira ine, m’bale. Aleluya!’” Ndiye iwe ukutenga zakudzilungamitsa wekha.

<sup>54</sup> Mulungu amayenera kuti azikupatsa iwe kenakake kakang’ono, kamodzi pakanthawi, kuti kazikhala ngati kakukufasitsa iwe apo pang’ono, inu mukudziwa. Ndiko kulondola. Uzikhala ngati uzizindikira iwe kuti Iyeyo ndiye

Bwana. O, kodi Iye si wodabwitsa? Inde, bwana, ulemerero basi!

<sup>55</sup> Kotero iye, Paulo, ndiye, atangotha kukhala ndi chomuchitikira chachikulu ichi . . .

<sup>56</sup> Tsopano, ngati izo akanakhala ali winawake lero, iwo akanamati, “O, Mulungu adalitsike, aleluya. Mnyamata, Ambuye andichitira ine chinachake! Ulemerero kwa Mulungu!” Koma osati Paulo; iye anali sikolala wa Baibulo.

<sup>57</sup> Chokuchitikira icho chiyenera kuti chigwirizane ndi Mawu a Mulungu. Inde, bwana. Ngati izo siziri zonse palimodzi zikugwirizana mu Baibulo . . . Osati kungoyang’ana *apa*, ndi kuti, “O, inde, ndi izi apa pomwe. Mulungu adalitsike, ine ndiri nacho Icho.” A-nha. Umo si momwe Mulungu amaperekera Izo.

<sup>58</sup> Izo ziyenera kumakhala ziri Baibulo lonselo, lonse Ilo. Chifukwa, inu mukhoza . . . Achikunja amagwiritsa ntchito Baibulo lomweli ngati bwalo lawo lochitirapo mtsutsano. Koma iwo amatenga Lemba laling’ono *apa*, kutembenezira apa ndi kukatenga laling’ono lina cha *apa*, kuyesera kuti awapangitse iwo kumangirizana palimodzi, ndipo ali maphunziro awiri osiyana, palimodzi. Kotero, inu muyenera kuti muzipangitsa Lemba kufanana ndi Lemba.

<sup>59</sup> Monga Yesaya ananena, mutu wa 28, “Izo ziyenera kumakhala mzere pa mzere, mzere pa mzere; apa pang’ono, apo pang’ono.” “Gwiritsani icho chomwe chiri chabwino.” Mukuona, umo ndi momwe Izo zimabwerera: mzere pa mzere pa mzere, Mawu pa Mawu, Lemba pa Lemba. Zonse izo ziyenera kumawunjikizana pamodzi. Ndicho chifukwa, ine ndikuganiza, mu maphunziro awa monga ife tikukhalira nawo tsopano, ndi chinthu chachikulu kwa mpingo, chifukwa icho chikuwabweretsa iwo pa malo pomwe Malemba onse akumangirizana pamodzi. Ndipo chotichitikira chatu chiyenera kumamangirizana ndi Lemba limenelo. O, ndi izi pano! Ngati izo sizitero, ndiye ndi zolakwika.

<sup>60</sup> Ndipo momwe ine ndinayendera kwa zaka, mosadziwa kuti Kuwala kumeneko kunali chiani kumene kunamukanthira Paulo pansa. Pamene, dziko lakunja, Malemba . . . Anthu, alirika ankayesera kumandiuza ine, “Izo ndi za Mdierekezi. Bwanji, iwe ukhala wambwebwe. Iwe ukhala wazamizimu. Usati upusitsidwe ndi Zimenezo, Billy. Chinachake ncholakwika ndi Zimenezo. Usati uzichita izo, mnyamata. Uko nkulakwitsa. Uyo ndi Mdierekezi. Chabwino, mnyamata, iwe ukhala waziwanda mwachizolowezi. Iwe ukhala wazamizimu ngati iwe uti uchite izo. O, zonse izo ndi za Mdierekezi. Ndizo—sindizo zolondola.” Koma pamene . . . Ine sindinkafuna kumalalikira izo.

<sup>61</sup> Koma monga pa msewu waku Damasiko, Paulo sankafuna kuti azilalikira izo, mpaka iye atapeza ngati izo zinali zolondola kapena ayi. Kotero iye anapita uko mu Arabia kwa

zaka zitatu, ndipo anakawaphunzira Malemba. Aha! Pamene iye anabwerako, iye anati, “Tsopano gwedezani izo zichoke kwa ine.”

<sup>62</sup> Iye ankadziwa kuti iye ankayenera kuti akakomanizane nawo Afarisi. Iye ankayenera kuti akakomanizane nawo Asaduki. Iye ankayenera kuti akakomanizane nalo dziko, ndipo dziko la Amitundu. Ndipo kotero Paulo, Baibulo Ili linalembedwa, Bukhu ili la Ahebri, linalembedwera kwa cholinga chimenecho. Iye akuwagwedeza Ahebri amenewo, ndi kutenga Chipangano Chakale icho ndi kuchisonyeza Icho kuno ku Chipangano Chatsopano. “Uyu ndi Mulungu,” iye anati, “apa izo ziri p—pa aneneri onse ndi chirichonse.” Zikuyambira mmbuyo momwe pachiyambi, mutu wa 1 ife tinali nazo, “Pakuti Mulungu mu nthawi zamakedzana, mmbuyo momwe mu nthawi zakale, mu machitidwe osiyanasiyana, ankayankhula kwa makolo kupyolera mwa aneneri.” Ndi momwe Mulungu ankabweretsera uthenga Wake, woyesedwa ndi Urimu Tumimu. “Koma mu tsiku lino wayankhula kwa ife kupyolera mwa Mwana Wake, Khristu Yesu,” zoyesedwa ndi Baibulo Lake. Ndi inu apo.

<sup>63</sup> Chotero zotichitikira izi zomwe dziko likuti, “O, ndi zamutu. Bwanji, palibe aliyense...” Pamene Mngelo uja anawonekera, Kuwala kuja kumusi kuja pa mtsinje, pamene ine ndinkalalikira chitsitsimutso changa choyamba kuno pangodya, ife tinawabatiza anthu onse aja. Ine ndikukhulupirira, M'bale Fleeman, inu muyenera kuti munali mu... Ine sindikudziwa ngati inu munali kuno apo kapena ayi. Ndi angati anali kuno p—pamene Kuwala kuja kunawonekera pa mtsinje? Kodi alipo akale aliwonse pano? Inde, ena a iwo. Pamene Iko kunatsika kuno pa mtsinje.

<sup>64</sup> Ndipo iwo anati, “Iko kunangokhala kuphidiguka kwa diso.” Ambiri a ife tinali titaima, tikuyang’ana pa Iko, ndipo apa Iko kunabwera pansu. Ndiyeno zaka mtsogolomo, Mulungu anatsimikizira Izo ndi diso lamakina la kamera. Ndi zoon.

<sup>65</sup> “Chabwino, kodi izo—ndi zopeka zina? Kodi izo ndi chinachake ch—chomwe...” Ayi, bwana. Ife tikuzitenga izo kuchokera mu Baibulo momwe umu ndi kukusonyezani inu. Ndi Ambuye Yesu yemweyo. Iye akuchita chinthu chomwecho. Kachitidwe Kake ndi komweko. Mphamvu Yake ndi yomweyo.

<sup>66</sup> Tapenyani, Lamlungu lapitali, kuno. Kutaliko, nditagona pa kama wanga, sindinayambe ndamuwonapo bamboyo mu moyo wanga. Kudza apo ndipo anati, “Kuli bambo ku kachisi, ndipo iye ndi wa imvi, wamutu-wakuda, laimvi. Iye ndi wakhungu, ndipo iye sangathe kuyenda. Iye ali mu chikuku. Bambo wa mutu wakuda amutumiza iye uko; dokotala, Dr. Ackerman, bambo wa mutu wakuda, bambo wa Chikatolika. Anamutumiza bamboyo, atakhala apo pomwe. Ndipo PAKUTI

ATERO AMBUYE, anawuka apo, anayenda natuluka ali ndi kupenya kwake ndi chirichonse. Nchiani chinachita izo? Pano pali Mngelo yemweyo. Mmodzi yemweyo yemwe anamukanthira Paulo pansi, ali panjira akupita ku Damasiko, akukhala mu Mpingo Wake ndi anthu Ake lero. Ndi Lemba kufanizitsa ndi Lemba. Umo ndi momwe izo zimayenera kumakhalira.

O, ife tiri ndi *ofunda*. Ife tilowa mu zimenezo, pakapita kanthawi.

<sup>67</sup> O, ife tiri ndi chinthu chakuya patsogolo pathu, ngati ife tingakhoze kungolowa mu izo, lero ndi usikuuno. Tsopano izo zikungoyamba kulowa mu madzi okuya. Komwe inu . . .

<sup>68</sup> Inu mukudziwa, pamene ine ndinali mnyamata wamng'ono, ine ndinkakonda kukhala ku dziwe laling'ono kuseri kwa malowo, ndipo ine ndinkapita kunja uko. Ndipo tonse ana aang'ono ife tinali kulowamo, maliseche; aang'ono, pafupi usinkhu wa zaka sikisi, seveni. Ndipo ife . . . Madziwo anali akuya pafupi *chonchi*. Iwo sanali kuposa posambira nkhumba. Ndipo ine ndinali ndi bokosi la sopo pamenepo. Ine ndinkasonyeza kuti ine ndinkakhoza kudumphiramo, nditagwira mphuno yanga, ndi kukhavula, ndi kumapita monga *choncho*. Ndipo mimba yanga yang'ono inkakhoza kugunda matope, inu mukudziwa, ndipo iwo ankakhoza kumangowulukira njira iliyonse. Ine ndinawauza adadi anga kuti ine ndimakhoza kusambira.

<sup>69</sup> Iwo ananditengera ine kubwerera kumeneko tsiku lina. Iwo anati, "Ine ndikufuna kuti ndikuwone iwe ukusambira." Ine ndinalumpha kuchoka apo, inu mukudziwa; ndinavula zovala zanga, kathengo kakang'ono ka dzombe; ndipo ndinathamangira mmusimo, ndinakagunda madzi. Ine ndinali ndikukhavula, matope akungowulukira paliponse. Ndipo bambo anali atakhala pa kamlatho. Iwo anakhala pamenepo ndi kumandiyang'anira ine kwa maminiti pang'ono. Anati, "Chokapo pa bowo ilo la madzi, ndi kukasamba, ndi kumapita kunyumba." Mukuona?

<sup>70</sup> Chabwino, njira yake ndi imeneyo basi, ena a ife omwe timadzitcha tokha Akhristu. Ife timakwawa-mmatope. Ndiko kulondola. Bola ngati iwe wazikika, "Ndine wa Methodist. Ndine wa Pentekoste. Ndine wa Presbateria. Ine ndiri nawo umboni; ine ndiri nawo Iwo." Iwe ukukwawa-mmatope.

<sup>71</sup> Tsiku lina ine ndinali ndi amalume anga. Ine ndinakhala ndikuwauza iwo . . . Iwo anali pafupi usinkhu wa zaka fifitini, sikisitini. Ife tinali ku mtsinje. Ine ndinati, "Amalume a Lark, ine ndimakhoza kusambira." Ndipo ine ndinali nditakhala kumbuyo kwa ngalawa, inu mukudziwa, ndinkamvera bwino ndi wotetezeka. Iwo anangotenga nkhamu ndi kundikankhira ine kutali, mu madzi a mapazi khumi. Apo zinali zosiyana

ndiye; kukhavula konseko, ndi kulira, komwe inu munayamba mwakumvapo mu moyo wanu.

<sup>72</sup> Tsiku lina inu mudzakankhidwapo, inu kuli bwino muzidziwa pamene inu mwaima. Inde, bwana. Ngati inu mukumudziwa Iye, inu muyenera kumamudziwadi Iye kwenikweni. Ndiko kulondola.

Koma tsopano ife tikupita mu madzi okuya, madzi okuya, komwe angakupangeni inu kumira ngati i—ngati inu simuli, Mkristu wabwino wonenepetsedwa.

<sup>73</sup> Zindikirani Mawu. Paulo, poyamba anapeza zimenezo. Iye anabwerera mu Chipangano Chakale, ndipo iye anapeza izi. Iye anawona chomuchitikira chake icho, mwamtheradi. “Tsopano kodi Icho chinali chiani chomwe chinandikanthira ine pansi?”

<sup>74</sup> Iko kunali Kuwala, Kuwala kwakukulu kutaima pamenepo, kukuwala ngati dzuwa, kutaima patsogolo pa nkhope yake. Iye anati, “Saulo, Saulo, chifukwa chiani iwe ukundizunza Ine?”

<sup>75</sup> Iye anati, “Ambuye, Inu ndi ndani yemwe ine ndikumuzunza?”

<sup>76</sup> Iye anati, “Ine ndine Yesu.”

<sup>77</sup> “Ine ndimaganiza Iye anali—munthu, wa dzanja la zipsyera, yemwe iwo akunena kuti akuwonekera mu misonkhano tsopano, ali ndi zipsyera za msomali mu manja Ake ndi mutu Wake.” Ayi, ayi; osati thupi *limenelo*, osati mu thupi *limenelo*. Mukuona? Iye tsopano ali Kuwala. Saulo . . .

<sup>78</sup> Pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi, Iye anati, “Ine ndinabwera kuchokera kwa Mulungu. Ine ndikubwerera kwa Mulungu.”

<sup>79</sup> Iye anali Mngelo yemwe ankatsogolera Ana a Israeli mu Kuwala uku, kudutsa mu chipululu. Iye anabwereranso ku Kuwala komwe komweko. Ndipo Paulo anakuwona Iko, kuchokera mu Chipangano Chakale. Iye anati, “Ine ndine Yesu, Mngelo wa Pangano.”

<sup>80</sup> Ndipo Iye anakhala thupi, kuti atiwohole ife. “Sanadzitengere mawonekedwe a Angelo,” ife tikupeza mu mitu yambuyomu, ife tiri . . . kuziphunzira. “Iye sanadzitengere konse chikhalidwe cha Angelo, koma anali Mbewu ya Abrahamu,” kuti Iye akhoze kumadziwidwa, kuti anthu akanakhoza *kumuwona* Mulungu. Amen.

Tsopano Iye akuti, “Ine ndibwereranso kwa Ilo.”

<sup>81</sup> Ndipo pamene Paulo analiwona Ilo, iye anati, “Zedi, uyo anali Iye. Uyo anali Iye.”

<sup>82</sup> Petro anali ndi chomuchitikira usiku wina pamene iye anali kupemphera. Kuwala uko komwe kunabwera mu nyumbayo, kunatsegula zitseko patsogolo pa iye, anapita kunja mu misewu. Ndipo Petro ankaganiza kuti iye anali kulota; iye

anali atadzozedwa kwambiri. Iye sankadziwa chomwe chinali chitachitika. Iye anati, “Kodi ine ndangodzuka kumene? Koma ine ndiri kunjja kuno pa msewu.”

<sup>83</sup> Ndipo iye anapita uko ku nyumba ya Yohane Marko. Ndipo msungwana wamng’ono anatsegula chitseko, dona wina wamng’ono uko, anali mu msonkhano wa pemphero. Winawake anali akugogoda pa chitseko. Anatsegula chitseko. “O,” iye anati, “ndi uyu Petro apa tsopano. Inu mukumupempherera iye kuti atuluke mu ndende. Ambuye amumasula iye.”

<sup>84</sup> “O,” iwo anati, “pita uko.”

“O Ambuye, amumasula iye!”

<sup>85</sup> “Bwanji,” iye anati, “iye waima pakhomopo, akugogoda.”

Petro anangopitiriza kugogoda, “Ndiloleni ine ndilowe.”

<sup>86</sup> “O,” iye anati, “ndi Petro.” Masiku amenewo, iwo anali nazobe, chitsulo chaching’ono chotsekera. Chivindikiro chaching’ono apa, iwe umatukulira mmbuyo ndi kuyang’ana kunjja, kuwona. Iwe usanamulowetse mkati mlendo wakoyo, iwe umayenera kuti udziwe yemwe akugogoda pa chitseko chakoyo. Chifukwa, iwo anali ndi okuba; ngati iwe utsegula chitseko, iwo akanati akuphe iwe.

<sup>87</sup> Kotero, iwo anatsegula chitseko. Iye anati, “Ndi Petro.”

<sup>88</sup> Iwo anati, “O! O, mai, iye wafa. Uyo ndi mngelo wake waima apoyo. Mukuona? Walowa kale mu thupi lake laulemerero, inu mukudziwa, fiofane iyo.”

<sup>89</sup> Mukukumbukira momwe ife tinatengera Izo, Daimondi yaikulu, momwe Iyo inkanyezimiritsira Kuwala, momwe Iyo inkabwererera uko? A... “Msasa wa pansi pano ukadzasungunuka, ife tiri nawo wina uli kutiyembekeza kale.”

Ndipo iwo ankaganiza kuti Petro anali atafa kale, thupi lakale ili linali litagwa, ndipo iwo akanaliyika ilo mmanda mu masiku angapo. “Iye anali atalowa mwa mngelo wake, kapena lake laul-...” Osati thupi laulemerero, koma mu fiofane yake, thupi lomwe liri lokonzedwa kale. Ilo silingakhoze kukugwirani chanza. Ilo liribe manja oti lizigwirira chanza, monga choncho, koma ilo liri mu thunthu la munthu. “Linabwera pansi, ndipo anali akugogoda pa khomo.”

<sup>90</sup> Iye anati, “Ayi. Ndi Petro. Iye waima pamenepo.” Iye anatsegula chitseko ndipo analowa mkati. Apo iye anali. Tsopano, Petro anali atawomboledwa ndi Kuwala uku.

<sup>91</sup> Tsopano, njira yomweyo imene woyambirira uja... Paulo uja, mu Mpingo woyambirira, anakuwona Kuwala kwa Mulungu kuja komwe kunawalira pa Paulo, Chinthu chomwecho chabwera pansi. Tsopano, anthu akhoza kunena chirichonse, izo sizimapangitsa icho kukhala cholondola. Koma pamene Mulungu atsimikizira chirichonse, ntchito ya



Icho imatsimikizira Icho. Ndiye, kamera ikutsimikizira Icho. Ndipo chirichonse chimene ife . . . chimene Ambuye wachichita, chakhala chiri mwamtheradi, chotsimikiziridwa mosalephera kuti Icho ndi Mulungu, mwa Malemba, mwa zochita Zake, mwa zokuchitikira. Koma iwo sangati amvetserere.

<sup>92</sup> Tayang'anani apa mu kachisi uyu. Tsopano, kumbukirani, inu mukudziwa izi. Ife sitikhumba chigulu. Ife tiribe malo oti tiwaikemo iwo, mulimonse. Koma, onani. Msonkhano wa mtundu uwu, pamene ife timabwera palimodzi kwa ichi, umayenera kukopa Mizinda ya ku Falls. Koma iwo ali okufa. Iwo ali okufa mwamtheradi. Iwo ali nawo maso koma iwo sakukhoza kupenya.

Inu mukuti, inu, “Bwanji, M'bale Branham, kodi iwo sangapite kwa dokotala ndi kukakonzetsa maso awo?” Iye sangakhoze kukonza kupenya kwa mtundu umenewoko.

<sup>93</sup> Yesu anati, “Ngati inu mukadandidziwa Ine, inu mukadalidziwa tsiku Langa.” Iye anati, “Inu Afarisi akhungu. Inu mumakhoza kuzindikira mawonekedwe a mlengalenga, koma zizindikiro za nthawi, inu simukukhoza kuzizindikira.”

<sup>94</sup> Kodi izo zikupita pamwamba pa mutu wanu? Mvetserani. Tayang'anani pa zizindikiro zomwe ife tikukhalamo kuno. Tsopano, izo si basi zina . . . Ine, mwiniwanga, ine ndangokhala munthu, osati nkomwe mlaliki, woti azikambidwa. Ine ndiribe maphunziro, a omwe dziko limachitcha, “mlaliki.” Ndipo ndife anthu osauka chabe. Tayang'anani pa nyumba yomwe ife tirimoyo. Tayang'anani pa makafiduro, mmawa uno. Koma taonani komwe Mulungu ali. Ndi chimenecho chinthucho.

<sup>95</sup> Choteronso Moabu anali ataima apo mu kunyezimira kwake konse ndi kukongola kwake, koma uko kunali Israeli mu mahema. Koma kodi Mulungu anali kuti? Uko kunali gulu la oyera-odzigudubuza apang'ono kumeneko, akuchita chirichonse chomwe chinali cholakwika. Koma Balaamu, wao—bishopu wao, analephera kuwona Thanthwe lokanthidwa lija, Njoka ya Mkuwa ija, Lawi la Moto lija. Maso ake anali akhungu. Iye sankakhoza kuliwona Ilo. Iye anati, “Iwo akungolingalira Ilo.” Koma Iye anali pamenepe.

<sup>96</sup> Mulungu adalitsike, o, Iye ali pano! Mulungu ali pano, ndipo Iye akuchita chinthu chomwecho chimene Iye anachichitapo. Ndipo Iye atero. Ife tikufanizitsa Lemba ndi Lemba. Mulungu sanayambe wadzilocha Iyemwini utoto wa chinachake chachikulu, pa dziko lapansi, koma Iye nthawizonse wakhala akukhala pakati pa anthu wamba ndi onyozeka. Ndipo pano Iye ali mmawa uno, akuchita chinthu chomwecho. Lemba likutsimikizitsira Izo. Kamera ikutsimikizitsira Izo. Tsopano, Icho, chifukwa chomwe ine ndikulozera ku chithunzi icho, si chifukwa chakuti ine ndiri pamenepe. I—ine ndangokhala wochimwa, wopulumutsidwa mwa chisomo, monga inu muliri.

Koma chimene ine ndikuyesera kunena, ndicho, Ndi Kukhalapo Kwake kuli ndi ife. Ndicho chinthu chachikulu. Chabwino, ngati Iye anandipanga ine e—Elisha mu thupi, ngati inu mukanakhala mulibe chikhulupiriro chokhulupirira izo, izo sizikanakuchitirani inu ubwino uliwonse.

“Iye anadza kwa Ake omwe. Ake omwe sanamulandire Iye konse.”

<sup>97</sup> Ndicho chifukwa, kuno mu mzinda lero. Pakuti, ine ndikanakhoza kuyambitsa chitsitsimutso kuno, mu nyumba ina yaikulu kapena chinachake, inu simukawapeza anthu ambiri amene akanakhulupirira izo. Iwo sangatero basi. Iwo sangakhoze. Tsiku lawo latha.

<sup>98</sup> Phunziro lomweli, mmawa uno, mu Afrika, likanakhoza mwinamwake kupereka zikwi khumi, mosachepera, miyoyo zikwi khumi kwa Khristu. Kapena, pakhoza kukhala pali wochimwa mmodzi atakhala pano mmawa uno, kapena chinachake, wobwererambuyo wina. Ambiri a iwo amangopesedwa mobwereza ndi kubwereza, mpaka izo zatheratu. Ndizo zonse.

<sup>99</sup> Koma chimene ife tikuyesera kunena, ndi, Lemba likufanana ndi Lemba. Tsopano, ziribe kanthu momwe chokuchitikiracho chiriri chachikulu, kupatula ngati chikufanana ndi Lemba, icho ndi cholakwika.

Urimu Tumimu, ziribe kanthu momwe mneneriyo analiri wabwino, ngati iye anayankhula ndipo kuwala uko sikunathwanimire pa Urimu Tumimu, izo zinali zolakwika. Momwe lotolo linkawonekera labwino, ngati ilo silinathwanimire pa Urimu Tumimu, ilo linali lolakwika.

Pamene unsembe uwo unatha, Mulungu anaika Baibulo lake apo. Paulo anati, “Ngati Mngelo wochokera Kumwamba akanabwera,” Agalatia 1:8, “ndipo akanati adzalalikire uthenga wina uliwonse kuposa umene walalikidwa kale kwa inu, musiyeni iye akhale wotembereredwa.”

<sup>100</sup> Mngelo wochokera Kumwamba ananena kwa Yohane mvumbulutsi, yemwe anali Mulungu Mwiniwake, “Ine Yesu ndamutuma mngelo Wanga kuti adzatsimikizitsire, kapena kuti adzasonyeze zinthu izi.” Iye anati, “Ngati munthu wina ati adzawonjezere mawu amodzi kwa Ilo, kapena kuchotsapo Mawu amodzi kwa Ilo, chimodzimodzi zidzachotsedwa mu Bukhu la Moyo, kwa iye.” *Ili* ndi Ilo, Baibulo.

<sup>101</sup> Chotero, zotichitikira izi ndi zinthu izi zomwe ife tiri nazo kuti zikuchitika kuno, ngati izo sizinali zitatsimikizitsiridwa ndi Mawu a Mulungu, izo zikanakhala ziri zolakwika; ine sindikusamala zomwe zikanati zichitike, izo zikanakhala ziri zolakwika. Kotero ndizo Mwamalemba, Choonadi mwamtheradi. O, ndine wokondwa kwambiri ndine membala wa Thupi lalikulu la Khristu.

<sup>102</sup> Tsopano, tiyeni tizipita tsopano, ife tikubwerano ku phunzirolo. Tsopano, ife tinatsirizira cha apa pamene iye anati, “Powona kuti ife tazunguliridwa tsopano...” Ine ndikupepesa. Ndizo, ine ndimabwereza mutu wa 12. Ine ndakhala ndikuwerenga izo, koma ine sindinaziphunzire izo. I...

<sup>103</sup> M'bale Norman, akukhala kunyumba uko, ndipo iye akudziwa kuti ine ndangobwerako kumene dzulo, ndipo abale akudziwa, kumusi uko, ine ndinangobwera kumene. Nthawi yokha yomwe ine ndinali nayo kuti ndiwerenge Lemba uko, inali nditakhala komwe kuno, maminiti angapo apitawo. Ndiko kulondola. Osamawaphunzira Iwo, ine ndimangoyembekezera Mpaka Mzimu Woyera uwapereke Iwo monga momwe Iye akufunira izo. Iye akudziwa komwe munthuyo a—ali, yemwe ayenera kukhala nawo Iwo. Chotero ngati ine nditi ndikhale nditapanga malingaliro anga choti ndichinene, ndiye izo nzolakwika. Koma ngati ine ndingomusiya Iye achite izo, Iye awutenga Iwo molunjika mpaka pa dontho pamene Iwo ukuyenera. Mukuona? “Musati muziganizira chomwe muti mukanene, pakuti Si inuyo yemwe amayankhula, ndi Atate Anu yemwe akukhala mwa inu. Iyeyo akuchita kuyankhulako.”

<sup>104</sup> Tsopano, mutu wotsiriza, mutu wathawo, ife tinamva izi, kuti, “Ife tidzathawa bwanji, ngati ife tinalanyaza chipulumutso chachikulu ichi; Chomwe chinayamba kulalikidwa kwa ife ndi Ambuye Yesu, ndipo Iye ndi iwo omwe ankamumva Iye?” Zinthu zomwezo zimene Yesu ankachita, kuti asonyeze, zinthu zomwezo zimene zikuchitika panozi: Mngelo yemweyo wa Mulungu, ntchito zomwezo, umboni womwewo, chirichonse chomwecho, chirichonse motsatira, Uthenga womwewo, limodzi ndi Mawu. “Ngati izo zinaphunzitsidwa ndi Ambuye, ndiye nkutsimikiziridwa ndi ophunzira Ake omwe ife tinawamva,” Paulo pokhala yemweyo, “ife tidzathawa bwanji, ngati ife tinalanyaza chipulumutso chachikulu choterocho?”

<sup>105</sup> Tsopano, Paulo anali kunena izo kwa omumvera ake a Chihebri. Tsopano, iwo analibe matepi rekoda, lero, monga ife tiri nawo kuno. Koma iwo anali ndi alembi omwe ankakhala apo, akulemba Izo apo pamene Paulo anali kulalikira Izo.

Ndipo ndizo zomwe Izo ziri pakali pano. Ife tikuzitenga Izo mwa matepi rekoda, ndipo matepi awa amapita kudziko lonse, mukuona, kuti asonyeze kuti Icho ndi Choonadi. Chipembezidzo chathu sichiri mwachabe, Icho ndi mwamtheradi Yesu Khristu wowukitsidwa, chinthu chomwecho. Tsopano ife tisamati tizichinyalanyaza Icho.

<sup>106</sup> Tsopano, inu musamati musingochokera ku mpingo, lero, ndi kuti, “Chabwino, ine ndimakhala ngati ndimasangalala kumapita uko. Ine ndimakonda kuimbako, ndipo anthuwo

ndi aubwenzi ku mpingo wawung'ono wakale uwo." Musati muzichita zimenezo.

<sup>107</sup> M'bale, muzilola mtima wanu uziyaka moto, kumati, "Pano, ine ndiyenera kuti ndichite chinachake pa izi. Ine ndiyenera kuti ndipite kunja kuti ndikawone ngati ine ndingakapeze winawake kuti apulumutsidwe."

<sup>108</sup> Ndipo musati muzipita uko, kumakati, "Mulungu adalitsidwe, ngati inu simulapa, inu muwonongeka." Ayi.

Zipitani pa izo mwaulemu. "Zikhalani wanzeru ngati njoka, wosapweteka ena ngati nkhunda." Mukuona, ndi momwe ungati uzipitira. Zimufikirani munthuyo, ngati iye akuweta nkukuku, muzikamba za nkukuzo, kwa iye, kwa kanthawi. Mukuona? Ndiyeno, chinthu choyamba inu mukudziwa, inu mukhala mukukamba za Ambuye. Ngati iye ali mlimi, zikambani za ulimi wakewo.

<sup>109</sup> Ngati iye amagulitsa magalimoto, zikambani za magalimoto akewo, kwa kanthawi, "Magalimoto abwino omwe inu muli nawo," ndi zina zotero. Mukuona?

<sup>110</sup> Mpaka inu mutaugwira Mzimu, pamene Atate ati, "Tsopano ndi nthawi yoti umufikire iye pa za moyo wake."

<sup>111</sup> Inu mukhoza kutsirizitsa izo, mukuona, "Iyo ndi galimoto yabwino. Inu mukudziwa mayendedwe, lero, akhala opambana. O, momwe mafuko abweretsedwera palimodzi moyandikana; ndipo mizinda ya mafuko athu, yayandikana palimodzi. Abwenzi ndi amathu akumakhoza kuyenderana wina ndi mzake. Inu mukudziwa, ndi chinthu chodabwitsa kukhala ndi magalimoto onga omwe inu mukugulitsawa."

<sup>112</sup> "Inde, bwana. Zedi izo ziri. U-nhu." Inu mukudziwa, akusuta ndudu yake, kapena chirichonse chomwe chiri. "Eya, awo, awo ndi magalimoto abwino."

<sup>113</sup> "Kodi inu munayamba mwaganizapo chomwe anthawi zakale akadaganiza ngati iwo akanawona chinachake chonga icho?" Basi kumangopitirira nazo munga choncho, inu mukudziwa.

Pakapita kanthawi, kuti, "Inde, eya, ndithudi ziri."

<sup>114</sup> Inu mukudziwa, chinthu china chomwe iwo akuchita, iwo akubweretsa munga ife tikamakhala nazo, ngati mu zitsitsimutso. Anthu akhoza kubwera kudutsa mu dzikoli, mwamsanga, ku chitsitsimutso." Mwaona, inu mukutsegula njira, nthawi yonseyo, inu mukudziwa.

<sup>115</sup> Ngati inu mumverera kuti Chinachake chikutsamwa pa njirayo, imirani apo pomwe, sunthirani cha *kuno*. Monga dotolo ananena, ku Phoenix uko, anati, "Ambuye, dzazani kamwa yanga ndi mawu abwino, ndiye ndigunyuzeni ine pamene ine ndanena zokwanira." Inu mukuona? Eya. "Ndigunyuzeni ine pamene ine ndanena zokwanira."

116 Tsopano, zindikirani tsopano, ife tikuti tiyambire pa mutu wa 15, kapena ndime ya 15 ya mutu wa 3, mwacheru tsopano.

*Pamene izo ziri kunenedwa, Lero ngati inu . . . mumva mawu ake, musawumitse mitima yanu, monga mwa kupalamula.*

117 Tsopano penyani Paulo akuyankhula apa. Tsopano izo zinanenedwa, “Lero, patapita nthawi yaitali chotero.” Ife tikuti tilowe mu izo pakapita kanthawi, kuti, “Lero, nthawi yaitali chotere.” Zikubwera mpaka mu mutu wotsatira, “Patapita nthawi yotalika chotere.”

*. . . izo zikunenedwa, Lero ngati inu . . . mumva mawu ake, musawumitse mitima yanu, monga mu tsiku la kupalamula, pamene iwo anamupalamula Mulungu.*

118 Tsopano tiyeni tiwerenge ndime yotsatira.

*Pakuti ena, pamene iwo anamva, anamupalamula: . . .*

Tsopano kodi iye akuyankhula za chiani? Uthenga.

*. . . komabe si onse omwe anatuluka ku Igupto ndi Mose.*

*Koma anali omwe Iye anakwiya nawo kwa zaka makumi anai? Kodi sizinali ndi iwo omwe anachimwawo, amene matupi awo adagwa mchipululu?*

119 Tiyeni tiime apa miniti. Kupalamula, “pamene iwo anapalamula.” Tsopano kodi Mulungu anachita chiani? Tsopano Paulo akuyesera kuyankhula. Ndi chiani Icho chomwe chinawatsogolera iwo potuluka mu Igupto? Kodi anali Mose? Ayi. Mose anali chida chathupi.

120 Tsopano ife tiri ndi maziko apa. Ife tikufuna tifike powongoledwa tsopano. Pamene ife titi tigunde pa malo awa apa, mu maminiti pang’ono, i—inu muziwona izo.

121 Tsopano, Mulungu anali ndi anthu Ake ali ndi mpumulo wosakhazikika. Iwo anali uko mu Igupto. Iwo anali atachoka pa malo awo oyenera. Iwo anali atachoka ku dziko lakwawo. Iwo anali alendo ndi ammwendamnjira, ndipo Mulungu anali woti awatulutse iwo kuchokera ku nyumba zosungidwamo, m—mu Igupto, kupita ku dziko lakwawo.

122 Choimira cha lero; ndife osakhazikika. Kuno sizimatenga nthawi. Ana amanja onenepa akusewera mabulo, asungwana aang’ono ali ndi zidole, akusewera; chinthu choyamba inu mukudziwa, iwe umakhala ndi tsitsi laimvi, ndipo utachita makwinya. Pali chinachake cholakwika apa. Kuno si kwathu. Ife tiri mu malo olakwika. Ndicho chifukwa ife tikuti ndife amwendamnjira ndi alendo. Chinachake chachitika.

123 Dona wamng’ono ananena, mmawa uno mu chipinda, za momwe anthu amamusekera iye, nthawi zina. Ine ndinati,

“Koma, mlongo, wokonedwa, iwe si wa anthu amenewo.” Ife ndi anthu osiyana.

<sup>124</sup> Msungwana wanga wamng’ono anati, “Adadi, asungwana *akuti-akuti* anachita zinthu *zakuti-zakuti* zomwe iwo amachita.”

<sup>125</sup> Ine ndinati, “Koma, taona wokonedwa.” Iwo anali ndi marekodi awa a Elvis Presley. Ine ndinati, “Ine sindikanawafuna iwo mnyumba mwanga.”

<sup>126</sup> Iye anati, “Koma, adadi, iwo ndi asungwana abwino aang’ono.”

<sup>127</sup> Ine ndinati, “Iwo akhoza kukhala ali. Ine ndiribe kanthu koti ndinene motsutsa izo. Koma pali chinthu chimodzi, ife ndife osiyana. Ife ndife osiyana. Osati kuti ife tikufuna kuti tikhale osiyana, koma Mzimu umene uli mkati mwathu wachoka ku zimenezo. Ndiwe wa mdziko lina.”

<sup>128</sup> Pamene ine ndipita ku Afrika, ine sindingafike pa kudzisinthira ku m—m—momwe iwo amakhaira moyo. Iwo samavala zovala zirizonse. Iwo amakhala amaliseche. Ndipo iwo amatola chinachake chomwe chiri chovunda, chiri ndi mphutsi mmenemo, iwo amadya icho, mulimonse; sizimapanga kusiyana kulikonse. Mukuona?

<sup>129</sup> Ndipo Izi ndi zosiyana. Inu mukudziwa, nthawi ina, ife tonse tinali monga choncho, koma chitukuko chatibweretsa ife ndi kutipanga ife mosiyana.

Ndipo kutembenezidwa kwachulukitsa izo ka milioni. Ife sitikufuna zinthu zovunda za mdziko panonso. Khristu watipanga ife kuti tikhale Akhristu; momwe chitukuko chatipangira ife kuti tikhale aukhondo. Ndipo zindikirani, osati icho chokha, koma ife tikudzinerera kuti ndife amwendamnjira ndi alendo. Ife sitiri a mdziko. Ndiye, inu simumafuna kanthu kochita nalo dziko. Ndipo zinthu zimenezo zapita kutali.

<sup>130</sup> Tsopano, Israeli anali uko mu Igupto. Iwo sanali Aigupto. Aigupto, chinali chamanyazi kuti wachi Igupto aike manja ake pa nkhusa. Ndipo Israeli anali oweta nkhusa. Ndipo momwe ziyenera kuti zinamufika Mose, pambuyo pa kulemekezeka konse kwa kukhala wachi Igupto, oweta ng’ombe.

Kodi inu munazindikira zomwe Farao ananena kwa Yosefe, ndi zina zotero? “Ilo ndi themberero.” Anati, “Abale ako ndi oweta nkhusa.” Ndipo ngakhale m’Igupto sakanakhoza kuika manja ake pa woweta nkhusa. Iye anali wa anthu osiyana.

<sup>131</sup> Ndipo umo ndi momwe izo ziriri ndi Mkristu, lero, pamene iye abadwa kachiwiri. Izo si. . . Ndi nyansi kuti iye aziyanjana nawo pomwe anthu akumwa ndi kumanena nthabwala zoipa, ndi akazi amaliseche. Ndi i. . . Icho, n—ndi zanyansi. O, adalitsike Ambuye! Ife ndi amwendamnjira kuno. Ife ndi alendo kuno. mzimu watembenezidwa, ndipo ife tikufunafuna

Mzinda kumene akazi samavala zazifupi. Ife tikufunafuna Mzinda kumene iwo samakhala ndi malo omwera mowa. Ife tikufunafuna Mzinda mmene mumakhala chirungamo. Koteru, ndife amwendamnjira.

<sup>132</sup> Chotero, Mulungu anatsika mu mtolo waukulu wa Moto, ngati Lawi, anausea pansi mu kathengo ndipo anayamba kudziulula Iyemwini kwa Mose, choyamba. Mose anati . . .

Inu mukudziwa momwe ife tinaliri ndi phunziro usiku wina, momwe kuti pamene Yesu anali kuno pa dziko lapansi, Iye anati, “Chabwino, asanakhalepo Mose, INE NDINE.” Uyo anali Yesu mu chisamba choyaka, mu Lawi Lamoto. Ndi Yesu, lero, yemweyo.

Ndipo Iye anadziulula Iyeyekha mu Lawi la Moto, ndipo Mose anapeza chomuchitikira. Iye akupita uko mu Igupto. Iye akukalalikira Uthenga, nkhani yabwino, ndipo zizindikiro ndi zodabwitsa zinamutsatira iye. Inu mukuzimvetsa izo? Chinthu chomwecho lero.

<sup>133</sup> Osati izo zokha, koma Ahebri awo anatuluka, anayenda mu Kuwala, iwo anali kutsogozedwa ndi Lawi la Moto lomwelo. Ndipo Baibulo linanena kuti, “Musati muzimuyesa Mulungu.”

<sup>134</sup> Penyani izi: Ndiroleni ine ndiwerenge Izi.

*Pamene zikunenedwa, Lero ngati inu . . . mumva mawu ake, musaumitse mtima wanu, mawu ake kuyankhula kwa mtima wanu, monga mu kumupalamula, pamene iwo anamupalamula Iye.*

Mvetserani.

*Pakuti ena, pamene iwo anamumva iye, anamupalamula: . . .*

<sup>135</sup> Ndi angati akudziwa kuti Aisraeli anamupalamula Mulungu ndi kusakhulupirira kwawo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi] Iwo anang’ung’uza. Iwo kwathunthu . . . Mulungu anayenda mpaka komweko. Ndipo pamene iwo anapeza zonse . . . Chinthu choyamba, iwo analowa mu vuto.

Apa panali Lawi la Moto ili pamwamba pawo. Ine sindikudziwa ngati iwo onse ankaliwona Ilo, kapena ayi. Bola, Mose analiwona Ilo. Ndipo Ilo linali pamwamba pa iwo, ndipo iwo ankaliyang’ana Ilo. Ndipo pamene iwo anabwera pansi . . . Titi ngati iwo sanaliwone Ilo, ine sindikudziwa ngati iwo analiwona ilo kapena ayi. Ilo linkapita patsogolo pawo. Baibulo linati Ilo linkakhala pamenepo.

<sup>136</sup> Ilo linati, “Nyenyenzi inkapita patsogolo pa amuna anzeru.” Palibe amene ankaliwona Iyo kupatula amuna anzeru. Iyo inkadutsa malo oyang’anira mmwamba aliwonse. Iwo ankasunga nthawi mwa nyenyenzi. Palibe yemwe ankaliwona Iyo kupatula amuna anzeru. Iyo inali kwa iwo kuti aziyiwona Iyo, ndipo amuna anzeru anali omwe Nyenyenziyo inatumizidwirako.

137 Ndipo Lawi la Moto linatumizidwira kwa Mose, ndipo Mose anatumizidwira kwa ana a Israeli. Ndipo iwo ankayenera kuti azimutsata Mose. Iwo ankakhoza kumuwona Mose, ndipo Mose ankawona Kuwala.

Pamenepo iwo ankapita!...?..Ndipo pamene iwo anali kutuluka, iwo anafika pa Nyanja Yofiira. Ndipo, o, i—iwo sankaziwona zizindikiro zonse izo za zozizwitsa ndi zinthu zikuchitika pamene iwo anali akadali m—mu dziko lakale la Igupto, koma pamene iwo anapita uko pa ulendo wawo, atatembenezidwa ndi kumatuluka. Ndiye, chinthu choyamba inu mukudziwa, iwo analowa mu vuto.

138 Mulungu amakonda kukubweretsani inu mu vuto. Iye amakonda kuika vuto pansi kuti awone chomwe inu muti muchite nalo. Kotero Iye anangoimitsa Nyanja Yofiira, ndipo chinthu choyamba inu mukudziwa, anawayendetsa iwo mpaka mu malo awa omwe, ndiye anamutuma Farao kuti awatsatire iwo. Mukuona momwe Mulungu amakondera kuchita izo? Iye amakonda kuti aziwonetsera mphamvu Yake ndi chikondi. Iye ndi Mulungu, ndipo Iye amangokonda kuti akusonyezeni inu yemwe Iye ali. Amen.

Ndipo vuto la izo ndi lakuti, lero, anthu amati, “O, masiku amenewo anapita.” Ayi. Mulungu angakhoze bwanji kudziwonetsera Yekha, pamene inu mukuphunzitsidwa zinthu ngati zimenezo? Koma Mulungu amakonda kuti azidziwonetsera Iyeyekha.

139 Apa ankabwera ana a Israeli, akuyenda mu Kuwala. Mose, akupitabe patsogolo pawo. Apo iwo anali, “Zibwerani. Njira yake ndi *iyi*. Mulungu akuitana. Ife tikutuluka. Ife tikupita ku dziko lolonjzedwa.”

“O, aleluya!” Apa iwo onse anali, akufuula, ndi kulumpha, ndi kukhala ndi nthawi yabwino, inu mukudziwa. Ndipo chinthu choyamba inu mukudziwa, iwo anayang’ana mmbuyo ndipo anati, “O, kodi fumbi ilo ndi chiani?”

140 Mmodzi wa iwo anakwera pamwamba pa phiri, nati, “O, o! Kalanga, kalanga! Ndi ankhondo a Farao.”

141 Mulungu anati, “Inu mukuchita mantha ndi chiani? Kodi inu simunakhulupirire zomwe Ine ndinachita kumeneko? Inu mukudandaula ndi chiani? Inu mukundikwiyitsa Ine chifukwa chiani?”

142 Pamene iwo anafika kumusi uko, Mose anachokapo ndipo anakafunsira kwa Mulungu. Mulungu anangotsegula Nyanja Yofiira ndipo iwo anayenda nawoloka; anamutsekera mdani mkati. Umo ndi momwe Mulungu amachitira izo. Musati muziwopsyzedwa. Musati musingotengeka. Musati muzikhumudwitsidwa. Inu mumupalamula Mulungu.



143 Ndiye kodi Iye anachita chiani? Zikuwoneka ngati, “Chabwino, ife tinali ndi yesero limodzi lalikulu; Mulungu adalitsidwe, ife tathana nazo izo. Ife sitikhala nawonso ena. Ife tiri pa njira yathu waku dziko lonjeredwa.” Ndipo Iye anawatsogolera iwo waku chipululu momwe, komwe kulibe madzi. Kodi inu mungalingalire? Mulungu, ndi A—ndi anthu Ake oyeretsedwa, opatulika, anawatsogolera iwo mpaka mu khwekhwe *ili* lomwe; ndiye anawachotsa iwo mu khwekhwe limenelo, ndipo anawatsogolera iwo mpaka kuno komwe kulibe madzi. Pamene Iye akanakhoza kuwatengera iwo njira ina komwe kunali madzi. Bwanji, Iye akanangopanga mtsinje, njira yonse motsatira, ngati Iye akanafuna kutero. Iye akanakhoza kuswa phiri lililonse kukhala lachisangalalo, kukhavulira madzi mapazi makumi asanu mu mlengalenga, ngati Iye akanafuna kutero. Zedi, Iye akanakhoza. Koma ngati Iye akanachita izo, izo zikanakhala zophweka kwambiri. O, mai! Lidalitsike Dzina la Ambuye.

144 “Chifukwa chiani Mulungu anazilola *izi* kuti zichitike, M’bale Branham? Nchifukwa chiani Mulungu?”

Mulungu akuchita zimenezo. Musiyeni Iye yekha. Zingoyendani chamtsogolo. Iyo ndi ntchito ya Mulungu. “Moponda mapazi a olungama mumatsogozedwa ndi Ambuye.” Inde, bwana. Zimapanga kusiyana kotani?

145 “Ndataya ndalama zanga zonse, M’bale Branham.” Chabwino, Mulungu adalitsike, chonchobe.

146 “O, ine ndachita *izi*, ndipo *izi* zachitika, mkhuntho unadzaiwulutsa nyumba yanga.”

147 Mulungu adalitsike, chonchobe. “Ambuye anapereka, Ambuye azitenga zachoka, lidalitsike Dzina la Ambuye.” Zipitirirani kumayendabe. Zonsezo ndi za kwa ulemerero wa Mulungu. Mulungu akudziwa zomwe Iye akuchita.

Ena kudutsa mmadzi, ena mnamondwe,  
Ena muyesero lakuya, koma tonse Mmwazi.

148 Umo ndi momwe Iye amatitsogolera ife. Ndiko kulondola. O, mai! Ine ndikumverera ngati ine ndingoima ndi kufuula. Umo ndi momwe Iye amawatsogolera ana Ake okonedwa. O, kodi inu mungangomverera . . . Tsopano, ine sindine wowerenga maganizo, koma kodi inu mungakhoze kungomverera Mzimu wokondeka uwo tsopano ukungosambitsa mu nyumba muno? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Bwanji ngati maso athu atatseguka pakali pano, ndi kupenya omwe aima kuzungulira mmbali mwa makoma awa, mmwamba-ndi-chotsika ndi timipita iti?

149 O Elisha! Mmawa wina, pamene mnyamata uja anangokhala wakhungu monga iye akanakhala ali, iye anati, “Tayang’anani pa Asiria kumusi uko.”

Anati, “Koma alipo ochuluka ali ndi ife.”

Anati, “Ine sindikumuwona aliyense.”

Anati, “Ambuye, tatsegulani maso a mnyamata uyo.”

<sup>150</sup> Iye anayang’ana pozungulira mneneri wokalamba uja, paliponse kuzungulira apo, mapiri anali ali pa Moto, ndi akavalo a Moto, ndi magaleta a Moto. Iye anakhutitsidwa ndiye.

<sup>151</sup> Iye anati, “Ife tingopita tikawakanthe iwo ndi khungu.” Iwo anali nako kupenya kwawo mwanngwiro basi monga iwo anali nako nthawizonse, koma iwo anali akhungu kwa iye. Anati, “Inu nonse mukumufuna Eliya?”

Anati, “Inde, bwana.”

<sup>152</sup> “Bwerani, ine ndikusonyezani inu komwe iye ali.” Ndipo uyo anali iyeyo, akuwatsogolera iwo. Iwo sankadziwa zimenezo.

<sup>153</sup> Umo ndi momwe izo ziriri lero. Khristu ali pano. Mzimu Woyera uli pano, ukuchita zinthu zomwezo zimene Iye nthawizonse amazichita, ndipo dziko ndi lakhungu kwa Izo. Iwo sakuzidziwa Izo. “O, i—ine sindikudziwa za Izo. Abusa anga . . .” O, anthu osauka olema! Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Iwo ali akhungu kwa Iwo. Iwo sakuwudziwa Iwo. Mulungu akutsogolera.

<sup>154</sup> Tsopano, iwo anabwera, kudutsa Mchipululu cha Tchimo, uko kunalibe madzi uko. Mulungu anangokhala nazo zonse zitaperekedwa. O, ndipo iwo anapeza chithaphwi cha madzi, iwo anati, “Awa ndiwo.” Ndipo iwo sakanati awalawe nkomwe iwo. O, iwo anali oyipa. Mai, i—iwo anali oyipa kuposa salfa zana pa zana. Mwaona, anali basi ngati mazira ovunda, inu mukudziwa. “O, mai! Ndi oyipa.” Iwo anali chiphe. Tsopano, chotchedwa Chipululu cha Tchimo. Mitengo ingapo ya mgwalangwa imamera kumeneko, ndi kasupe kumene migwalangwa imeneyo imamera. Ndiye Mose anati, “Musati . . .”

<sup>155</sup> Mulungu anati, “Chifukwa chiani iwo? Chifukwa chiani iwo? Kodi iwo akundipalamulira chiani Ine? Chabwino, ngati Ine ndinachita *zijazi* kumbuyo uko, kodi Ine sindingathe kuchita chinachake pomwe ziri chonchimu?”

<sup>156</sup> Ngati Iye anakudutsitsani inu kamodzi pa nthawi yodwala, kodi Iye sangakuchotseni inu pa kwinako? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Iye atakudutsitsani inu mu vuto lina, kodi Iye sangakuchotseni inu mu linalo? [“Ameni.”] Mulungu adalitsike! Ngati Iye anandichotsa ine mu tchimo, Iye akhoza kudzanditulutsa ine kuchokera mmanda. Iyeyo ndi Mulungu. Zingapange kusiyana kotani? Zingopitirirani, ikani maso anu pa Iye.

<sup>157</sup> Anati, “Ngati ine ndinaitseka Nyanja Yofiira mmbuyo, ndi kuwamiza Aiguto aja, kodi ine sindingakhoze kuchita chinachake ndi madzi awa? Chifukwa chiani inu mukundikwiyitsa Ine? O, kusakhulupirira kwanu!

Inu mukundipalamula Ine kuti ndikwiye, chifukwa cha kusakhulupirira.”

<sup>158</sup> Tsopano mawu apa omwe akugwiritsidwa ntchito ndiwo, “Tchimo,” anapalamulila. Anapanga...Chifukwa chomwe iwo anachitira izo, iwo sanakhulupirire. Iwo sanatuluke ndi kukayamba kuwombera chandamale, tsopano, ndi zinthu monga choncho. Iwo sankayendayenda ndi mkazi wa mwini wake, ndi kumapita ndi kumakanena bodza. Izo sizinali zomwe iwo ankachita. Koma, izo si tchimo, pa kuyamba pomwe.

<sup>159</sup> Kukhala moyo wa chigololo si tchimo. Kusuta, kutafuta, kumwa, njuga, kutukwana, kulumbira, zina zotero, izo si tchimo. Izo ndi zotsatira za kusakhulupirira. Iwe umachita zimenezo chifukwa ndiwe wosakhulupirira. Ngati iwe uli wokhulupirira, iwe sumachita zimenezo. Ndicho chifukwa Yesu anati, “Iye amene amva Mawu Anga ndi *kukhulupirira* pa Iye yemwe anandituma Ine, ali nawo Moyo wosatha.” Osati *akuti* iye akhulupirira, koma akukhulupirira kwenikweni! Apo izo ziri. Izo zimachotsera umboni wanu woyambirira kutali. Mukuona? Tsopano, ndi inu apo.

Osati, “Iye amene amva Mawu Anga ndi kumafuula.” Osati, “Iye amene amva Mawu Anga ndi kuyankhula ndi malirime.” Osati, “Iye amene amva Mawu Anga ndipo akakhala ndi magazi mu dzanja lake kapena pa nkhope yake,” kapena zina zonse zowonjezera. Izo si Zimenezo.

“Iye amene amva Mawu Anga nakhulupirira pa Iye yemwe anandituma Ine, ali nawo Moyo Wamuyaya, ndipo sadzafika konse ku Chiweruzo, koma wadutsa kuchokera ku imfa wapita ku Moyo.”

<sup>160</sup> Kodi tchimo ndi chiani? Kusakhulupirira. Kenakake kakang’ono kakhocha kuwukapo, mmalo moti mupite molunjika ku Lemba ndi kukapeza ngati Izo ziri zoono kapena ayi, “O,” inu mumati, “Ine ndiri...Ay! Taonani, apo, inu zipitirirani nazo. “Ine ndizingopitirira wa Chipresbateria monga ine ndiriri, mukuona.” Zipitirirani nazo, akhungu, ndipo inu mumamupalamula Mulungu.

<sup>161</sup> Pamene Mulungu achita chirichonse, iye amayembekezera kuti fuko lichigwire Icho. Koma, mmalo mwa izo, “Inu mukudziwa, chabwino, ine sindikudziwa za Izo.” Mukuona? Iye amayembekeza kuti anthu azimvetse Izo. Ngati inu mwakhuzidwa mokwanira, khalani pansu ndi Lemba. Dutsani mwa Iwo ndi kukawafufuza Iwo, mmbuyo ndi mtsogolo, ndi kuwona ngati Izo zinachitika, ngati Izo zinanenedweratu kuti zidzachitika, ndi zina zotero. Ndiye inu muzimvetse Izo. Amen.

<sup>162</sup> Tsopano zindikirani.

*Pamene ilo liri...Lero ngati inu...mumvere mawu ake, musati muwumitse mtima wanu, monga mu*

*kumupalamula*, pamene Mulungu anapalamulidwa ndi iwo, inu mukuona.

*Pakuti ena, pamene iwo anali atamva, anamva uthenga umene Mose ankalalikira, anamupalamula: ngakhale ziri chomwecho si onse omwe anatuluka mu Igupto ndi Mose.*

<sup>163</sup> Ndi angati akudziwa anthu angati omwe anapulumsidwa kuchokera mu gulu lapachiyambi lija lomwe linatuluka? Ndi angati? [Wina akuti, “Awiri.”—Mkonzi.] Awiri, ndi kulondola. Ndi angati akudziwa maina awo? [“Kalebu ndi Yoswa.”] Ndiko kulondola. Kalebu ndi Yoswa, awiri okha, kuchokera pa mamilioni awiri nchinachake.

<sup>164</sup> Mvetserani kwa izi. “Koma iye . . .” Ndime ya 17 tsopano.

*Koma omwe iye anakwiyitsidwa nawo kwa zaka makumi anai, chifukwa cha kusakhulupirira. Kodi izo sizinali ndi iwo omwe anachimwa, sanakhulupirire . . . ?*

<sup>165</sup> Tengani dikishonare ndi kupeza chomwe *tchimo* limatanthauza. Tengani dikishonare ya Baibulo. Ndi kusakhulupirira. *Kusakhulupirira* ndi “*tchimo*.” “Iye amene sakhulupirira ali woweruzidwa kale,” Yohane Woyera 4, mukuona, “waweruzidwa kale.”

*. . . omwe matupi awo anagwera mu chipululu?*

*Ndipo kwa omwe iye analumbira kuti iwo sadzalowa mu mpumulo wake, . . .*

<sup>166</sup> Kusakhulupirira kwano! O, momwe ine sinditi ndifikire ku mutu wanga. Koma, penyani, ndilo lomwe liri vuto ndi fuko lino, lero. Zizindikiro ndi zodabwitsa zadutsa fuko lino. Kodi iwo akuchita chiani? Mopitiriza atembenezira nsana wawo kwa Iwo. Ndipo Iye anati, “Ine ndikulumbira kuti Ine sindidzawalola iwo kukalowa mu Dziko lomwe iwo anayamba kupitako.”

<sup>167</sup> Vuto ndi chiani ndi mipingo yaikulu iyi lero? Kusakhulupirira kwawo kwamupalamula Mulungu. Aleluya! Iye ndi wokhoza mwa miyala iyi kudzutsira ana kwa Abrahamu. Iye anayesera kuti apereke Uthenga kwa iwo, ndipo iwo anawumitsa mitima yawo. Iwo anadzipangira okha miyambo, ndipo iwo anapanga zipembedzo zazing’ono, “Ndipo ife tikukhulupirira *izi* ndipo osati china chirichonse,” ndipo Mulungu sangakhoze kulowamo. Kodi iwo ali pati lero? Ali pa mzere wa pambali.

<sup>168</sup> Gulu lapang’ono, lokhulupirika la Mulungu likusunthirabe motsatira, ndi zizindikiro ndi zodabwitsa. Iye akuwaika iwo pa yesero. “Mwana aliyense yemwe abwera kwa Mulungu ayenera ayambe wayesedwa ndi kupimidwa,” kuphunzitsa-mwana.

<sup>169</sup> Kanthu koyamba kakang’ono komwe kachitika, “O, chabwino, mwinamwake palibe kanthu kwa Izo, mulimonse.” Ndiwe mwana wapathengo, ndipo osati mwana wa Mulungu.

170 Pakuti mwana wa Mulungu ali Mbewu ya Abrahamu, yemwe ankazitcha zinthu zimenezo zomwe panalibe, ngati kuti izo zinalipo, “Mulungu ananena chomwecho,” ndipo amangokhala akusunthira mtsogolo. Amen. Ziribe kanthu zomwe anena, kapena chirichonse chosiyana, iwo amakhala akusunthira patsogolo, mulimonse. “Mulungu ananena chomwecho.”

171 Zaka twente faifi iye anayembekezera mwana ameneyo, ziribe kanthu momwe zinaliri zosiyana. Ndipo iye anadzimatula yekha kwa osakhulupirira awo, ameni, chotero kuti iye akhoze kumakhulupirira. O, mai! Ine ndikumverera mwachipembedzo.

Taganizani za izo. Inu muyenera kuti muzidzipatula nokha kwa mbalume iyo ya mdziko, “Aha, masiku a zozizwitsa awo anapita. Palibe chinthu chotero chonga Izo. Uko ndi kutentheka.” Dzipatule wekha.

172 Baibulo linati, “Chokani pakati pawo, ndi kukhala inu mutadzipatula, atero Ambuye, ndipo ine ndikulandirani inu.” Kudabwitsa kwakeko! “Ine ndikulandirani inu, mukadzilekanitsa kaye nokha. Inu mukhala ana anga. Ine ndikhala Mulungu wanu. Dzipatuleni nokha. Musati mudzimange goli nokha ndi osakhulupirira.” Ndiko kulondola.

173 Mnyamata akamakwatira, kukwatira msungwana wina yemwe sakhulupirira; kapena msungwana wina kukwatiwa ndi mnyamata yemwe sakhulupirira. Musati muzichita zimenezo. Ine sindikusamala kaya mnyamatayo ndi wowoneka bwino chotani, n—ndi, kapena msungwana wooneka bwino chotani, ndi maso aakulu awo omwe iye ali nawo; iwo onsewo adzazirala limodzi la masiku awa. Koma, m’bale, solo yako idzakhala moyo kwa nthawizonse. Inu muzisamala zomwe inu mukuchita. Msungwanayo si wokhulupirira weniweni, kapena mnyamatayo si wokhulupirira weniweni, musati mudzimange goli nokha monga choncho. Khalani kutali ndi zoterozo. Izo zidzakuyambitsani vuto mu njirayi.

174 Tsopano mveterani, ndime ya 17.

*Koma . . . omwe iye . . . kodi iye anakwiyitsidwa nawo zaka makumi anai? kodi izo sizinali ndi iwo omwe anali atachimwa, omwe matupi awo anagwera mu chipululu?*

*. . . kwa omwe iye analumbira kuti iwo asadzalowe mu mpumulowo, . . .*

175 Iwo anayamba kutuluka, koma iwo anawona zozizwitsa, koma iwo sanakafike konse ku dziko lolonjzedwa. Chiwerengero chosankhika chokha, cha awiri, anakalowa mu dziko lolonjzedwalo.

176 Tsopano kodi Paulo akuchita chiani? Iye akuyankhula kwa Akhristuwo tsopano, “Musati mulole Uthenga womwewu, umene unalalikidwa mmbuyo kutali, mwa zizindikiro ndi zodabwitsa, ndipo Lawi la Moto linkawatsogolera iwo; pamene

zinthu izi ziti zizidzakachitika kachiwiri, musati inu mugwere mmphepete mwanjira, mwa kusakhulupirira, kuti mupite ku kukaikira, pakuti matupi awo anagwera mu chipululu.”

<sup>177</sup> Tsopano ife tikubwera mkati, mofulumira tsopano. Penyani mwatcheru.

. . .koma kwa iwo omwe sanakhale moyo?

*Chotero ife tikuwona kuti iwo sakanati alowemo chifukwa cha kusakhulupirira.*

Iye akulitcha ilo *tchimo* kamodzi, iye akulitcha ilo *kusakhulupirira* nthawi yotsatira. *Kusakhulupirira* ndi “*tchimo*.” “Iwo sanalowemo ayi, chifukwa cha kusakhulupirira kwawo.”

<sup>178</sup> Iwo ankamuwona mneneri uyo, Mose. Iwo ankawona zomwe iye ankachita, ankawona zomwe iye ankanena. Izo zinali zoono, nthawi iliyonse, ankayenda pa Choonadi chomwe. Lawi Lamoto ili linkakhoza kuwonekera patsogolo pawo. Iwo ankaliyang’ana Ilo. Iwo ankaliwona Ilo.

<sup>179</sup> Paulo, akuyesera kuti apeze, kenako, anafika pansu apa, pa chomuchitikirira chomwe iye anali nacho. Mukuona? Akuyesera kufotokoza chomuchitikiracho, iye anafanizitsira icho kwa Chipangano Chakale. Iye anati, “Tsopano ife talowa mu chinthu chatsopano, ku nyengo yatsopano iyi, mwa Yesu Khristu. Nthawi zakale, Ambuye ankawonekera kwa iwo mwa aneneri, koma tsopano Iye ali mwa Mwana Wake, Yesu.” Mukuona? Ndipo iye akupita, kuti afanizitse zomuchitikirazo ndi kuwasonyeza iwo zomwe zinali kuchitika, momwe zizindikiro ndi zodabwitsa, ndi chirichonse, ndi zomwe zinalembedwa.

<sup>180</sup> Tsopano iye anati, “Iwo sanalowe ayi, chifukwa cha kusakhulupirira kwawo.” Iwo sanakhulupirire.

<sup>181</sup> “Koma tsopano, ife, ife tikusunthira mu nyengo, ndipo inu musati muwumitse mtima wanu. Musati muchite momwe iwo anachitira, mu masiku a kumupalamula, pamene iwo anamupalamula Mulungu.” Kodi iwo anachita motani izo? Osati pa kukhala mopanda makhalidwe. Ndiroleni ine ndiperere izi pansu kwa inu.

<sup>182</sup> Inu mukuti, “M’bale Branham, ine ndimapita ku tchalitchi.” Izo ndi zabwino. “Ine sindinayambe ndanamapo mu moyo wanga.” Ndizo zabwino. “Ine sindinayambe ndabapo. Ine sindinayambe ndachitapo *izi, izo, kapena zinazo.*” Izo ndi zabwino kwambiri. Izo ndi zonse zabwino. Koma, izobe si *tchimo*.

<sup>183</sup> *Tchimo* ndi pamene Mulungu adzisonyeza Iyeyekha ndipo inu nkusazikhulupirira Izo, inu osafuna kumvetsera kwa Izo.

<sup>184</sup> “O,” inu mukuti, “mpingo wanga sumaphunzitsa Zimenezo.” Bola ngati Baibulo limaphunzitsa Izo, ndipo Mulungu nkumazitsimikizira Izo, ndicho chinthucho.

Tsopano yang'anani mphindi yokha. Tsopano ife tikuti tiyambe tsopano pa chinachake chenicheni, chakuya kwenikweni. Tsopano, ikani chikumbumtima chanu mu thumba lanu la chikhotho mpaka inu mutatuluka kunja.

185 Tsopano penyani mwatcheru kwenikweni.

*Tiyeni ife kotero tizichita mantha, kuwopa kuti,  
lonjezo litisiya ife kuti tikalowe mu wake. . .*

Wake mwamuna, wake mkazi, mapuronauni aumunthu tsopano. Chiani?

. . . aliyense wa inu angawoneke woperewera kwa ilo izo.

186 Tsopano, Paulo amayesera kuti awauze iwo, mu mutu wammbuyomu, za zinthu zonse izi. Koma tsopano iye akuyesera kuti awauze iwo chomwe Izo ziri.

O, kodi ife tiri nayo nthawi? I . . . Mwinamwake ife tibadikira mpaka usikuuno. Kukuda, ndipo ife tikhala ndi utumiki wa pemphero. Mwinamwake ife tizigwire izo usikuuno, chifukwa izi ndithudi ndi zodzaza ndi mavitameni, mavitameni auzimu. Tiri ndi zambiri zoti tichite, ndipo ine ndiri wotanganidwa madzulo ano. "Tiyeni ife . . ."

*Tiyeni ife chotero tichite mantha, kuwopa, lonjezo. . .*

187 Tsopano, kodi iwo anali nalo lonjezo la dziko lolonjezedwa, uko mu Igupto? Ndipo, pamene, Mulungu anabwera pansu, kuti adzapange lonjezo ili kukhala chenicheni. Bwanji, Mulungu anamuza Abrahamu, mazana ndi mazana a zaka mmbuyo, kuti Iye amati adzazichite izo. Izo zinali Mwamalemba.

188 Yosefe anati, "Musati inu mudzachotse mafupa anga kuchokera kuno mpaka inu muzidzapita ku dziko lolonjezedwa ilo ndipo mudzakandiike ine kumeneko ndi makolo anga onse." Chifukwa, iye ankadziwa kuti chiwukitsiro chinali kubwera, pamene Yesu ankauka kwa akufa, chifukwa iye anali atadziwa zomwe Yobu ananena. Mukuona?

189 Aliyense wa aneneri amenewo ankadziwa basi zomwe mneneri wina anali atanena, ndipo ankadziwa kuti Mzimu wao unali wofanana. Ndipo iwo anali kuyang'anira. O, m'bale! O, izo zikuyenera kutigwedeza ife nkutichotsa mu chikhalidwe chathu chachidziko. Iwo anali nawo maso awo, osati pa zomwe anthu anali kuyankhula, koma zomwe aneneri awo ananena. Aliyense wa iwo anali kuyang'anira.

190 Abrahamu anati, "Mudzandiike ine komwe kuno komwe Yobu anaikidwa." Anati, "Sara, ine ndikukagula chidutswa cha malo. Ife tizidzaikidwa komwe kuno."

191 Isaki anali mneneri, pambuyo pa bambo ake. Anati, "Mvetserani. Musati inu mudzandiike ine kwina kulikonse, osati

kuno mu Igupto, koma inu mudzanditengere ine kubwerera ku dziko lolonjezedwa. Inu mudzandiike ine komwe kuno.”

<sup>192</sup> Yakobo anafera mu dziko lolonjezedwa, koma ananena kwa mwana wake, yemwe anali mneneri, anati, “Iwe ukudziwa, usiku wina Mngelo anandikhudza ine pambali. Ine ndakhala ndikutsimpahina kuyambira pamenepo. Bwera, dzayike dzanja lako...” O, chifundo! “Mwana wanga mneneri, ndine wokalamba ndipo ndine wakhungu. Koma ika dzanja lako lopatulika, pokhala mneneri iwemwini, liyike ilo pa malo omwe Mngelo anaikapo dzanja Lake, ndi kulumbira kwa Mulungu wa Kumwamba kuti iwe sudzandiika ine kunoko.”

<sup>193</sup> Akhale wodala! Apo! Inu mukuliona vumbulutso lauzimu la Mawu? Bwanji, theka la iwo, pafupi magawo nainte pa zana, sankadziwa zomwe iye anali kuzinena. Koma iye ankadziwa zomwe iye ankazinena. “Dzaike manja ako a mneneri pa malo omwe Mngelo anaika dzanja Lake. Ine nthawiyina ndinali bambo wamkulu, wojintcha, wamantha wonenepa. Koma, Iye anandikhudza ine, ndipo kuyambira pamenepo ine ndakhala munthu wotsimpahina. Koma ine ndakhala ndiri kalonga kuyambira pamene ine ndinatsimpahina. Kuyambira pamene ine ndinasintha kayendedwe kanga, ine ndakhala ndiri kalonga.” Inde. “Ika dzanja lako apa. Ulumbire kwa Mulungu wa Kumwamba, iwe sudzandiika ine kuno.” Bwanji? Palibe yemwe ankadziwa zomwe iye anali kuzinena. Yosefe anadziwa. Iye anati, “Mudzanditengere ine kutsidyako ndi kudzakandiika ine mu dziko lolonjezedwa ilo.” Uko ndi kumene izo zinali. Ndithudi.

<sup>194</sup> Pamene Yosefe anafa, zaka mtsogolo, iye anati, “Musati mudzandiike ine kunoko. Koma inu muzidzayang’ana pa mafupa anga pamene muzidzadutsa apo, chifukwa tsiku lina inu mudzachokako kuno. Ndipo pamene inu muzidzapita, mudzatenge mafupa anga limodzi nanu.”

<sup>195</sup> Ndi inu pamenepo. Lisiyeni dziko linene zomwe iwo akufuna kutero, ndi kuchita zomwe iwo akufuna kutero. Lidalitsike Dzina la Ambuye. Ndisiyeni ine mwa Khristu, ngati ine ndikutchedwa chirichonse... wotentheka, kapena woyera wodzigudubuza. Tsiku lina Iye akubwera, ndipo iwo omwe ali mwa Khristu Mulungu adzaza nawo limodzi ndi Iye, pamene Iye akubwera. Izo zonse ndi Choonadi, choululidwa mwauzimu chiri apo pomwe, ndipo izo zimatengera malingaliro auzimu kuti agwire Izo. Kapumuleni pa izo, kudutsa tsikulo. Kaganizeni za izo. Ngakhale inu mukhale opanda kudya madzulo, kaganizeni za izo.

<sup>196</sup> Ndipo usikuuno, ife tilowa mu Mpumulo Wake, umene unasiyidwa, ndi kuwona chomwe lonjezo ili liri lero. Kodi chinthu ichi ndi chiani lero? Ngati Mulungu alibe Icho pano mu Baibulo, ndi kutsimikizira Icho, kuti Icho chiri apa pomwe



tsopano, ndiye ndine mneneri wabodza. Ndizo ndendende kulondola. Koma Iko kuli pano. Kodi Mpumulo uwu ndi chiani?

197 Iye anati:

Tsopano, *tiyeni ife...tichite mantha, kuwopa, lonjezo anatisiyira ife* kuti tilowe umo monga iwo anachitira,...

198 Ndipo Ilo liyenera kukhala lonjezo lomwelo. Uyenera kukhala uli mpumulo womwewo. Iye ayenera kukhala ali Mulungu yemweyo. Izo ziyenera kukhala ziri zizindikiro zomwezo. Icho chiyenera kukhala chiri chinthu chomwecho. Koma tiyeni ife tipumule. Tsopano kodi Iwo ndi chiani? Ambuye atapereka iwo kwa ife, usikuuno.

Pamene ife tikuweramitsa mitu yathu.

199 Ambuye wodala, Muyaya wokha udzaulula zinthu zazikulu zomwe ife tsopano tikugawana palimodzi. Mochepa . . .

Ndi ambiri omwe anadzozedweratu ku chiwonongeko. Monga Inu munanenera mu Bukhu la Yuda, kuti, “Amuna akale, odzozedweratu ku chiweruzo, akanati atenge chisomo cha Mulungu wathu ndi kuchisandutsa icho kukhala zazikhumbo.” Ndipo ambiri lero akulalikira Uthenga, chisomo cha Mulungu, ndi kuchipanga Icho kukhala dongosolo lopangira ndalama, kukhala ndi mpingo waukulu kwambiri ndi ochuluka mu Sande sukulu, kutenga chisomo cha Mulungu ndi kuchisandutsa Icho kukhala zazikhumbo. Ndipo dziko liri lakhungu, ndipo likumayenda ngati nkhumba zakhungu. Iwo Sali kumvetisa.

200 O Mulungu, tsegulirani kwa ife kumvetisa. Mulole kumvetisa kwathu kusakhale konga kwa ana a mdziko lino. Pakuti Inu munanena mu Mawu Anu, kuti, “Ana a dziko lino ali anzerupo kuposa ana a Kuwala.” Pachiyambi izo zinali chomwecho, “ana a Kaini” anakhala akatswiri aakulu asayansi. Iwo akukhala ophunzitsa aakulu. Iwo akukhala ogwiritsa ntchito zipangizo. Iwo amapitirira nako kutukuka, achipembedzo kwambiri, koma iwo anaweruzidwa ndipo anamizidwa mu chiweruzo. Ndipo matupi awo anayandama pa madzi, ndi miyoyo yawo inapita ku hade.

201 Ndipo Yesu anapita ndipo anakayankhula kwa iwo, pamene Iye anafa. “Ndipo anapita ku hade ndipo anakalalikira kwa miyoyo yomwe inali mu ndende, yomwe siinalape mu kupirira kotalika, mu masiku a Nowa,” limatero Lemba. Ndipo Mulungu, pamene Iye anaima pa dziko lapansi, Iye anati, “Monga zinaliri mu masiku a Nowa, chomwecho zidzakhala ziri mu kudza kwa Mwana wa munthu.”

202 Koma ife tikuzindikira, “m’badwo ndiye wa Seti,” amuna odzichepetsa, amuna enieni a Mulungu, osadziwa zochuluka kwambiri za zinthu za mdziko, osasamala kanthu ka zinthu za mdziko, koma anaika kumbali kulemedwa kulikonse ndipo

anakhulupirira Mulungu, ndipo anakhala aneneri ndi amuna aakulu mu Ufumu. Pamene enawo, dziko lachipembedzo linalo, linkawaseka iwo, ndi kuwanyoza iwo. Koma ora linafika pamene kusefukira kwa madzi ndi chiweruzo zinadza.

<sup>203</sup> Chomwecho izo zinali mu kudza kwa Yesu Khristu. Momwe iwo ankasekera ndi kumunyoza Iye, pamene iwo anali ndi zipembedzo zawozawo ndi mipingo yawo yaikulu. Koma iwo anali kuinyoza Nyenyezi Yammawa, ndipo ankamuseka Iye. Komabe iwo analowa mu chiweruzo. Ndipo pamene iwo anathawa napita ku Yerusalemu, uko iwo anakadya ana awo omwe, chifukwa cha njala, ndipo magazi awo anayenderera mpaka mu zipata za msewu pamene iwo anawotcha mzindawo ndi kachisi, ndipo miyoyo yawo inapita mu hade.

<sup>204</sup> Ambuye, pano ife tiri kachiwiri, pa wachitatu. Ino ndi nthawi yamoyo. Firii ndi chiwengero cha kuwala. Ndipo pano ife tiri, okonzekera Mkwatulo.

Mpingo ukusunthira mtsogolo, dziko la sayansi yaikulu. Mipingo lero yadzaza ndi okhulupirira-mokaikira. Makumi a zikwi ali ndi maina awo pa bukhu, inde, mamilioni, ndipo amaseka pa Uthenga, ndi kunena, kuti, “Iwo ndi osaphunzira. Iwo sakudziwa.”

Mwinamwake izo ziri chomwecho, Ambuye, koma chimene ife tikuchisowa mu maphunziro, Inu mumachikwaniritsa mu chisomo; pa kumutumiza Mngelo Wanu wa Kuwala, pa kuwonetsera mphamvu Yake, kutsimikizira Mawu kwa iwo omwe ali osauka ndi osaphunzira monga ife. Koma ife timakukondani Inu chifukwa cha izi, chifukwa ndi chisomo cha Mulungu chomwe chachita izi, ndipo ife tikudziwa kuti ife tinabadwa. Ndipo ife sitiri okondeka, konse. Ndife osakondeka kwambiri. Koma Inu, kupyolera mu chisomo, munafikira pansu ndi dzanja Lanu lachifundo ndipo mwawatsegula maso athu, monga Yesu anatipempherera ife; monga Eliya anachitira kwa Gehazi, pamene iye anayang’ana kuti awone pomuzungulira iye. Ndipo lero maso athu atseguka, ndipo ife tikuwona zinthu za Mulungu, ndipo ife tikudziwa kuti tikuyenda pa nthawi yotsiriza; pamene masiku a anthu Amitundu atsala pang’ono kuti atsirizike, ndipo Iye adzawatengera anthuwo kwa Dzina Lake. Tiyeni ife tikhale tikuwengeredwa mmenemo, Ambuye, modzichepetsa ife tikupempha. Ife tikupempha kuti Inu mupereka izo.

<sup>205</sup> Tidalitseni ife. Mudalitse omvetsera apang’ono awa mmawa uno. Iwo ndi opangidwa ndi mitundu yonse yosiyana ya zipembedzo ndi tizikhulupiriro, koma aiken iwo pambali lero, Mulungu. Ndipo mulole iwo ayang’ane molunjika cha ku Kalvare, nati, “Mulungu, ndiwumbeni ine ndi kundipanga ine. Ine ndiri monga...” Mneneri ananena kuti iye anapita ku nyumba ya wowumba, kuti iye akhoze kuswedwa ndi

kuwumbidwanso. Tiwumbeni ife ndi kutipanga ife monga mwa mawumbidwe awo omwe Mulungu angatifunire ife. Ziribe kanthu ngati ife tichita kukhala mphasa ya pansu ku Nyumba ya Ambuye. Ine kulibwino ndikhale chopondera pakhomo kuposa kumakakhala mu mahema ndi oyipa. Ndipo perekani izo, Ambuye. Ingotidalitsani ife tsopano, ndi kutisunga ife mochepetsedwa. Lolani mitima yathu ikhale yotseguka, malingaliro athu oyera, kwa zinthu za Mulungu, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Khristu.

<sup>206</sup> Ndi mitu yathu yoweramitsidwa, ine ndikudabwa ngati winawake angafune kuti akumbukiridwe mu mawu a pemphero, pofuna chipulumutso chanu kwa moyo wanu? Kodi inu mungakweze dzanja lanu, ndi wochimwa basi? Mulungu akudalitse iwe, mnyamata. Wina wakenso? Mulungu akudalitseni inu, kumbuyo uko, bwana. Mulungu akudalitseni inu, dona. Wina wakenso akufuna kuti akumbukiridwe mu pemphero pakali pano, kwa moyo wanu? Mulungu akudalitseni inu, bwana, ndi dzanja lanu mmwamba. Ndipo Mulungu akudalitseni inu, ndi inu apa. Zodabwitsa. Kodi pangakhale winanso, basi tisanatseke? Ine ndikumverera pangakhale. Mulungu akudalitseni inu, kumbuyo uko, bwana, kumbuyoko.

<sup>207</sup> Titi, tsopano penyani, ine ndikufuna kuti ndikufunseni inu chinachake. Ine sindikufuna kuti inu muziganiza konse chifukwa ndi kachisi wamng'ono uyu. Ine sindikufuna kuti inu muziganiza kuti ndi chifukwa chakuti ndi anthu awa. Ndipo Mulungu wochulukira chifundo, musati muganize kuti Mngelo wa Ambuye yemwe anajambulitsa chithunzi Chake ndi ine, ndi ine. . . n—ndi chinachake cha chimenecho, kuti achite zimenezo. O Mulungu! Ngati ine ndikanamverera mwanjira imeneyo, ndiye, m'bale, ine ndisowa kuti ndikakhale pa guwa mmalo moti ndizikufunsani inu. Koma ine ndikungonena izi, ine ndikungonena izi mwa Lemba, kuti inu muwone kuti ichi ndi Choonadi. Ngati ine ndinanena Icho, ndipo izo nzonse zomwe zinali kwa izo, ndinapitirira nazo monga mlaliki wina aliyense kapena winawake mzake, kapena wina aliyense, chabwino, ndiye, izo zikanakhala zosiyana. Koma inu mukuwona chinthuchi, Mulungu amabwera kumene pozungulira ndi kudzatsimikizira kuti ndi Choonadi. Mukuona? Ndi chimene chimapangitsa Icho kukhala chenicheni, ndi Mulungu kutsimikizira Izo. Ndiyeno, osati izo zokha, koma Mawu Ake amanena kuti Iye adzachita zimenezo. Pano Iye akuchita izo.

<sup>208</sup> Tsopano ngati inu simuli mu cholondola, mtima wanu suli mwabwino ndi Mulungu, kodi inu mungangokweza dzanja lanu? Nkuti, “Ndipempherereni ine.” Chabwino, pomwe inu mulipo. Pafupi manja asanu ndi atatu kapena khumi akwera mmwamba, akufuna chifundo kwa moyo wawo. Pamene inu muli ndi mitu yanu itaweramitsidwa, tsopano inu mupemphere.

Kumbukirani, inu ndi yemwe woti mulape. Ine ndikungofunsa chifukwa cha inu, kuti Mulungu akuchitireni chifundo. Koma ilo ndi guwa, Mulungu wakubweretsani inu pa malo mu malingaliro anu; limenelo ndilo guwa. Ife timakhulupirira za kubwera ku guwa, zedi, koma izi si—izo si. . . Izo ndi zabwino. Koma guwa lanu lenileni ndi pamene Mulungu anakomana nanu. Ndipo Iye wakomana nanu inu pamene mwakhala pomwepo. Ndilo guwa lanu.

<sup>209</sup> Tsopano itini, “Mulungu, ndichitireni ine chifundo, wochimwa. Ndipo kuyambira tsiku lino kupitirira, ngati Inu muti mundithandize ine, ine ndizikakhalira moyo Inu. Ine ndi—ine ndizikutumikirani Inu. Ine sindikusamala zomwe wina aliyense anganene, ine ndikubwera patsogolo, mmawa uno. Ine ndikupemphera pomwe pano, ndipo Inu tengani mzimu wakale wosatatiza uwu uchoke pa ine. Inu muchotse kupsyamtima uku kwa ine. Ine ndikudziwa ine sindingamachite monga chomwecho ndi kukhala moyenera ndi Mulungu. Ndipo ine ndiri ndi udani mu mtima mwanga. Ndine wansanje. Ine ndiri ndi njiru. Ine ndiri ndi *ichi, icho*. Zichotsenimo izo, Mulungu. Ine sindikufuna kuti ndikhale monga choncho. Ndipangeni inu wokoma, ndi wodzichepetsa, ndi wofatsa. Ndipangeni ine wofatsa. Ndipangeni ine munthu woteroyo kuti ine ndizikhoza kupindulira ena kwa Inu. Ndiroleni ine ndizikuchitirani Inu chinachake kuti ndisonyeze kuyamikira mu moyo wanga.” Ndilo pemphero lomwe inu muzilipemphera tsopano, pamene ife tikupemphera limodzi.

<sup>210</sup> Atate Akumwamba, iwo ndi Anu. Iwo ndi zipatso za Uthengawu mmawa uno. Iwo anakweza dzanja lawo. Chinachake chinawapangitsa iwo kuchita izo. Iwo, iwo ananyoza malamulo a mphamvu yokokera pansu pamene iwo anakwezera mmwamba manja awo. Apo panali mzimu mwa iwo womwe unapanga lingalirolo. Iwo anakweza mmwamba manja awo, kuti iwo amamuvomereza Mlengi yemwe anawapanga iwo.

<sup>211</sup> Tsopano, Atate Akumwamba, ine ndikupemphera kuti Inu muwadalitse iwo, ndi kupereka kwa iwo Moyo Wamuyaya, pakali pano. Palibe chomwe ine ndingakhoze kuchita; kuwaitanira iwo kudzazungulira guwa, kuwaika iwo mu chipinda chapadera, kuchita ntchito yonse. Izo, izo zimatengera Inu kuti muchite izo, Ambuye. Ife sitingakhoze kuchita zinzano kuposa kulalikira Mawu. Inu munati, “Chikhulupiriro chimadza pakumva, kumva kwa Mawu, Mawu a Mulungu.” Tsopano, ife talalikira Mawu, ndipo iwo akweza manja awo, kuti iwo akuwakhulupirira Iwo. Tsopano apatseni iwo Moyo wosatha, chifukwa Inu munalonjeza kuti Inu mudzachita izo. Ngati iwo anali odzipereka mu kukweza kwa manja awo, iwo atuluka mu chipinda chino mmawa uno, Akhristu okoma, ofatsa, odzichepetsa, chifukwa Inu munalonjeza izo. Ndipo Mawu Anu

sangakhoze kulephera. Ine ndikupempha izo mu Dzina la Yesu Khristu. Amenii.

Tsopano ndikuyang'anira, kudikirira ndi kukhumba,  
Mzinda wowala, Yohane anawona ukutsika.

Mu Mzinda wowala, (zimupembedzani tsopano), Mzinda woyera wangale,  
Ine ndiri nayo nyumba, zeze ndi nduwira;  
Tsopano ndikuyang'anira, kudikirira ndi kukhumba,  
Mzinda wowala, Yohane anawona ukutsika.

<sup>212</sup> Kodi inu simukungomukonda Iye? Uthenga watha, tsopano. Uku ndi kupembedza. Ife sitimangobwera ku tchalitchi kuti tidzangomva uthenga. Ife timabwera kuti tidzapembedze. Ingomuiwalani munthu ali pafupi ndi inuyo. Zingomupembedzani Iye. O, kukongola kwakeko! Kudabwitsa kwakeko! Ingomuuzani Iye mwanu... Inu simukusowa kuti mumuuze Iye mokweza. Ingomuuzani Iye mu mtima mwanu, "Ine ndikukukondani Inu, Ambuye. Ndikhululukireni ine tchimo langa." O, mai!

... Mzinda woyera wangale,  
Ndiri ndi nyumba, zeze ndi nduwira;  
Tsopano ndikuyang'anira, kudikirira ndi kukhumba.  
Mzinda woyera, Yohane anawona ukutsika.

<sup>213</sup> Atate athu, Mulungu, tilandireni ife. Ife tikuyembekezera, pamene ife tikumvetsera pa Mawu, kukhumba. "Mitima yathu ili ndi ludzu lofuna Inu, monga gwape afunira mtsinje wa madzi. Moyo wathu uli ndi ludzu lofuna Inu, O Mulungu." Kukhumba ndi kudikirira, kuyembekezera ora ilo ndi pamene Yesu ati adzaze, kuyembekezera nthawi yomwe ife titi tidzaitanidwire ku mlengalenga. Osati kuti tikaime pamaso pa Woweruza mu chiweruzo; izo zinadutsa kale. Ndife okufa ku zinthu za mdziko. Talowa mwa Khristu, ndipo Iye anatenga chiweruzo chathu. Iyeyo ndi Wotiyimira mlandu wathu tsopano, pa mpando wa chirungamo. Wotiyimira mlandu wathu wodala, yemwe, pa kuvomereza kwathu, Iye amachonderera mulandu wathu mpaka ife timadziwa kuti ndife osayenera. Monga mlongo wokonedwa wachikulire mmawa uno, ananena mu umboni wake, ndi kuika umo makobidi ake, "Kuchokera pomwe ine ndinabwera kuno ine ndaphunzira kuti Icho si chiyero changa, ndi chiyero cha Mulungu."

<sup>214</sup> Zoonaa, Ambuye, ife timawaphunzitsa anthu, mulibe kanthu kabwino mwa munthu, palibe chinthu chimodzi. "Munthu ndi chiani kuti Inu mumalingalira za iye?" Koma ndi chisomo cha Mulungu chomwe chawonekera kwa ife. Ndipo ife tikudalira mu zomuyenera Zake zokha, osati mu zathu zathu. Ndipo ife

tikukupembedzani Inu, Mulungu Woyera Kwambiri, chifukwa cha ubwino Wanu, pa kutiwerengera ife mu Ufumu Wanu waukulu, mu madongosolo Anu aakulu. Ife tikukulandirani Inu mu mitima yathu, mwa chikhulupiriro. Ndi mwa chisomo, ife tikukhulupirira kuti Inu mwapereka izo kwa ife kwa ulemerero wa Mulungu, kwa utumiki wa kwa Mulungu.

<sup>215</sup> Tsopano, Ambuye, achizeni odwala pamene iwo akubwera kuti adzapemphereredwe, mmawa uno. Perekani kwa iwo chisangalalo icho, chomwe iwo akhala akuyembekeza kuti akhale bwino. Lolani iwo adziwe kuti kuzunzika pang'ono uko, kopepuka komwe kunaikidwa pa iwo, ndi nthawi yaing'ono ya kuyesa. Mulungu akudziwa zonse za izo. Iye anachita izo kuti awone chomwe ife tikanati tichite ndi izo. Momwe Mulungu. . . Aloleni iwo abwere apo pomwe mmenemo ndi kutenga ntchito yotsirizidwa iyo! Mulole Inu. . . Mulole iwo asakupalamuleni Inu, pothamanga *apa* ndi *apo*, ndi *mkati* ndi *kunja*, “Chabwino, ine sindikudziwa *izi, izo.*”

<sup>216</sup> Ambuye, aloleni iwo atenge maimidwe owongoka, nkuti, “Ambuye, Inu munali Yemwe munandipulumutsa ine. Inu munali Yemwe munandichitira ine zinthu izi. Ine ndikukhulupirira Inu, ndipo ine ndikudalira Inu, lero.” Ndipo ine ndikupemphera kuti Inu mupereke izo kwa anthu, mu Dzina la Khristu. Amen.



*BUKHU LA AHEBRI*

Mauthenga khumi ndi umodzi awa a M'bale William Marrion Branham, anaperekedwa mu Chingerezi kuyambira Ogasiti 21 kudutsa Seputembala 22, 1957, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., anatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nadindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2009 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)